

M'BADWO WA MPINGO WA SMURNA



Atate a Ulemelero kwambiri, ndife okondwa kwambiri usikuuno kudziwa kuti tiri nawo Moyo wosafa mwa ife. Moyo wa Mulungu wathu wopatulidwa ndi malirime a moto ndi kudzakhala pa aliwonse a iwo, ndipo iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo anayamba kuyankhula ndi malirime ena monga Mzimu umawapatsira iwo zoyankhula. O Atate, momwe ife tikukuthokozerani Inu kuti Inu munadzigawaniza Nokha pakati pa Mpingo. Nzosadabwitsa Ambuye wathu anati, “Tsiku limenelo inu mudzazindikira kuti Ine ndiri mwa Atate, ndi Atate mwa Ine, Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine.” Momwe Mulungu Wakumwamba amadzakhala pakati pa anthu Ake! “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu mpaka kumalekezero a dziko lapansi.” Kutsika kudutsa m’badwo wa mpingo uliwonse Inu mumadzakhala kuno, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndipo ife nkumakudziwani Inu ndi ntchito zimene Inu mukuchita. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

² Ambuye, powona—powona chimake cha mibadwo yonse, nthawi ikukonzekera kutha ndipo Umuyaya wayamba kulowamo. Atate Mulungu, ndife okondwa kwambiri kudziwa kuti tikukhala mu tsiku la wotsalira uja lero; kuyang’ana miyoyo yathu ndi kuwona mtundu wa zolinga zimene ife tiri nazo, zolinga zimene ife tiri nazo, ndi kuwona kuti Mzimu Woyera watenga ulamuliro. Mulungu, mulole munthu aliyense mu Kukhalapo Kwaumulungu usikuuno azindikire mibadwo ya mpingo iyi imene ife tiri kukhalamo ndipo athawire mwamsanga kwa Ambuye Yesu, chifukwa izo zinalembedwa momveka bwino, kuti, “Dzina la Ambuye ndi nsanja yamphamvu, olungama amathawira mwa Iyo ndipo amakhala otetezeka.”

³ O Mulungu, bwerani usikuuno ndipo mudzadzoze umunthu wathu, Ambuye. Abweretseni oyendayendawo, O Ambuye, omwe asokonezeka kwambiri; yang’anani pa nkhosa yosauka, Ambuye, iwo sakudziwa choti achikhulupirire; kuitana kwa abusa kulipo konsekonse. Ife tikupemphera, Atate, kuti iwo akamumvere M’busa wamkulu uyo wa nkhosa, Ambuye Yesu, Mzimu Wake waukulu ukuyankhula usikuuno, ukuti, “Mwana Wangwa, bwera kwa Ine ndipo Ine ndidzakupatsa iwe Sabata, Mpumulo umene ukusindikizire iwe kopita kwako Kwamuyaya.” Osati kumangokankhidwira uku ndi uko pa dziko lapansi pamene ife tikuwona kuti nthawi ikutha tspano. Perekani izi, Atate.

Yankhulani kudzera mwa wolankhulayo, mvetserani kudzera mmakutu a iwo omwe akumva, pakuti ife tonse tikumvetsera. Mu Dzina la Yesu ife tikupemphera. Amenii.

⁴ Mukhoza kukhala pansii. Tsopano, usikuuno ife tikuphunzira mu m'badwo wa mpingo wachiwiri. Ine ndikuwawona ambiri a iwo akulemba zolemba ndi zinthu, ndipo ndi chifukwa chake ine ndikufuna kuti ndizizipanga izi kukhala zomveka nthawi iliyonse.

⁵ Tsopano, m'badwo wa mpingo wachiwiri unatchedwa m'badwo wa mpingo wa Smurna. Ndipo iwo unakhalapo, M'badwo wa Smurna, unayambitsidwa nthawi yomweyo imene M'badwo wa Efeso unatulukira. M'badwo wa Efeso unayambira A.D. 55 mpaka A.D. 170. M'badwo wa Smurna unabwera mu 170 ndipo unapita mpaka ku 312. Mpingo uwu ndi mpingo wozunzidwa; umene ukuvala korona wa ofera, ndi mpingo wa chisautso. Ndipo lonjezo la Mulungu kwa iwo, kwa Mpingo Wosankhidwa mmenemo, linali loti awupatse iwo korona wa Moyo.

⁶ Mpingo uliwonse unali ndi *nyenyezi* imene inkasungidwa mdzanja la Mulungu, imene inkaimira “wa mthenga” kwa m'badwo wa mpingo umenewo. Wopambana yemwe ndikhoza kumuganizira kuti anali mtumiki ku m'badwo wa mpingo wa Efeso (chifukwa Baibulo silimanena kuti iwo anali ndani) anali Paulo; chifukwa iye anakhazikitse mpingo wa Efeso ndipo anali mtumiki wa m'badwo wa mpingo umenewo; amene anabweretsa Kuwala kwa Mpingowo, umene Yohane Woyera anawutenga iwo kuchokera pamenepo. Ndipo kenako Polekapu, ndi kumapitirira mpaka mmusi . . . Polekapu, kani, mpaka mmusi.

⁷ Tsopano, M'badwo wa Smurna, ine ndikukhulupirira ndi zonse . . . zimene ine ndakhoza kuzipeza, anali Ireniasi. Ndipo tsopano ine ndikufuna kuti ndikupatseni inu chifukwa chimene ine ndinamusankhira Ireniasi mmalo mwa Polekapu. Tsopano, pafupifupi azibusa onse amafuna kuganiza kuti (ndi aphunzitsi a Baibulo) mngelo ameneyo anali Polekapu. Polekapu anali wophunzira wa Yohane Woyera, izi ndi zoonaa. Ndipo Polekapu anasindikiza . . . iye—iye anali wofera, iwo anamubaya iye pamtima ndipo anamupha iye. Tsopano, koma iye anali munthu wopambana, munthu wodziwika, munthu waumulungu, wokoma. Sindikukaikira mmodzi wa Akhristu aakulu kwambiri omwe ife tinakhalapo nawo. Ndipo panalibe chirichonse chimene inu munganene chotsutsana ndi moyo wake.

⁸ Chifukwa chimene ine ndinamusankhira Ireniasi: nchifukwa chakuti ine ndikukhulupirira kuti Ireniasi anali pafupi kwambiri ndi Lemba kuposa momwe Polekapu analiri. Chifukwa Polekapu ankatsamira pang'ono ku lingaliro la Chiroma lakuti akhazikitse bungwe. Ndipo—ndipo Ireniasi anali wolimba potsutsana nazo izo, iye mwamtheradi ankazitsutsa izo.

Ndipo kenako, monga ife tonse tikudziwira, nkhani yayikulu inali ikubwera ku Nicene Council; imodzi ya nkhani zazikulu inali yakuti ngati Mulungu anali *atatu* kapena Mulungu anali *mmodzi*. Ndipo Ireniasi anatenga mbali yakuti Mulungu anali Mulungu, tsopano, Mmodzi yekha.

⁹ Ine ndikhoza kuwerenga kuchokera mu *The Ante-Nicene Fathers*, mpukutu wa wani, tsamba 412, chobwereza chaching'ono chabe; ngati mukufuna kuti mulembe zimenezo, mpukutu wa wani wa *The Ante-Nicene Fathers*. Ndipo pa tsamba la thwelofo, ndipo ndi... Ngati inu mukufuna mpukutuwo, ndi gawo lotsiriza la mpukutu wa firii. Inu mukhoza kuwerenga chinthu chonsecho; alipo machaputala angapo a zimenezo, kapena ziganizo zingapo. Tsopano ine ndiyamba kuwerenga pamapeto kumene—pamapeto kumene pa twente, ndime sarte ya izo. Ine sindiwerenga izo zonse, koma gawo chabe la izo:

“Zoyankhula zina zonsezo chimodzimodzi kukhala... zikutulutsa udindo wa Chinthu chimodzi ndipo chomwe chomwecho;” (Onani, iye akuyesera kunena zomwe iwo ankamutcha Iye, 'Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,' ndipo iye anati, “Ndiwo *maudindo*, osati maina, maudindo a Munthu Mmodzi.” Izi ndizo ndendende zomwe ife tikuphunzitsabe mpakana lero.) “monga, mwachitsanzo” (ndiyeno ndizokutiridwa) “(mu Chingerezi), *Ambuye Wamphamvu, Ambuye Atate wa onse, Mulungu Wamphamvuzonse, Wammwamba Kwambiri, Mlengi, Mpangi*, ndi zina zotero. Awa si maina ndi maudindo olowezana a zinthu zosiyanasiyana, koma a chimodzi ndiponso chomwe chomwecho,” (Ameni!) “mwa dzina limene Mulungu mmodzi, Atate, ali... Iye—Iye amene zinthu zonse izi... anapereka kwa onse... za kukhalapo, zabwino za kukhalako konse.”

¹⁰ Ireniasi akunena kuti “Maudindo onsewa akuwonkhetsedwa mu Dzina limodzi, pansu pa Mulungu mmodzi, ndipo iwo ali maudindo chabe a zomwe Iye anali.” Iye anali Rozi la Sharon. Ndicho chimene Iye anali. Umenewo ndi udindo. Iye anali Nyenyezi Yammawa. Iye anali Alpha. Iye anali Omega. Amenewo ndi maudindo a chimene Iye anali. Iye anali Atate. Iye anali Mwana. Iye anali Mzimu Woyera. Koma alipo Mulungu *mmodzi*. Mulungu mmodzi, ndipo Dzina Lake ndi Limodzi. Ndipo ndicho chifukwa chimodzi chimene ndimaganiza kuti Ireniasi amalondola mu kwake—mu kuwunikira kwake apa, kapena kutanthauzira kwa Lemba.

¹¹ Chinthu china chimene ine ndikufuna kuti ndikuwerengereni inu, chikupezeka mu bukhu: *How Did It Happen?* Ndipo ili ndi la azambiriyakale. Ndipo, *How Did It Happen?* lolembedwa ndi R. C. Hazeltine, mbiriyakale ya mipingo yoyambirira. Ndipo apa pa tsamba 180: “Mphatso Zauzimu Mu Nthawi ya Ireniasi, A.D. 177 mpaka 202.” Tsopano,

chifukwa chimene ine ndikubwerezera izi, zikupita pa tepi, inu mukuona, ndipo—ndipo izo zidzachotsedwapo ndi kukaikidwa pa mabuku:

“Munali mu nthawi ya Ireniasi momwe mpingo waukulu wa Atumwi ku France unali ndi mphatso zonse za Mzimu Woyera.” Izo zinachokera ku kuphunzitsa kwa iye, mwaona. “Mamembala a mpingo wa Ireniasi ku Lyon,” kumeneko ndiku Lyon, France, “anayankhula ndi malirime. Izo sizinali zachirendo kumuwona munthu wakufa akuukitsidwanso ku moyo. Machiritso anali—mchiritso anali zochitika za tsiku ndi tsiku muulaliki wonse. . . mmipingo ya uvangeli konsekone.” Ireniasi ameneyo ankadziwa kuphunzitsa! “Zozizwitsa zinkachitika pafupipafupi. Kunena zoon, mipingo imeneyo siimakha yopanda mawonetseredwe a chozizwitsa a kukhalapo kwa Mulungu mwina mwa masomphenya, kuyimitsidwa kwa zinthu zachirengedwe, mozizwitsa, kuti awakumbutse Akhristu a uvangeli za tsiku lija, limene iwo anali ophunzira Ake okonedwa. Koma kuchokera ku mbirizakale zammbuyomu, ife sitingathe kukunkha chochitika chimodzi cha kuukitsa wakufa mu mpingo woyamba wa Roma.”

¹² Ndiwo anthu omwe samati. . . samakhala ndi chidwi ndi mbali iliyonseyo, iwo amangonena zowona. Ndi azambiriyakale.

¹³ Ndi chifukwa chake ine ndikuganiza kuti Ireniasi, chifukwa, inu mukuwona, anali ndi chikhulupiro chofanana ndi chimene Paulo ndi ophunzira ankachipereka. Ndi chifukwa chake ndiri. . . ndikukhulupirira kuti anali mngelo wa mpingo wa Smurna, chifukwa iye anali. . . iye anali ndi zophunzitsa zomwe zomwezo za Mwamalemba; ndipo kuphunzitsa kwa Mwamalemba kofanana pa maziko a Mawu a Mulungu kumabereka chinthu chofanana nthawi iliyonse. Ngati inu mutangotenga mophweka ndondomeko ya Mulungu ndi kukaichita iyo mpaka pa lemba, ziribe kanthu zimene mipingo ikunena, kungozitsatira izo mmene izo zinanenera, izo zidzabereka chinthu chomwe chomwecho. Ndiipo ndi zimene Ireniasi ankachita.

¹⁴ Tsopano, ine ndikuganiza kuti Polekapu anali munthu wabwino, mumvetse; koma ine ndikunena kuti iye ankatsamira kwambiri kuti awupange bungwe mpingo, ndipo mofanana ndi momwe Achinikolai ankachitira. Iwo amawupanga bungwe mpingo, ndipo—ndipo amabweretsa ubale pamodzi. Zomwe zimawoneka zabwino mwaluntha, koma, inu mukuwona, Mzimu umakhala patsogolo kwambiri pa luntha mpaka. . . inu simungaganizenso moyenera kwa—kwa Mzimu. “Malingaliro Anga apamwamba ndi okwera kwambiri kuposa malingaliro anu,” atero Mulungu. “Njira Zanga ndi zoposa njira zanu.” Chotero pali njira imodzi yokha yochitira izo; ingomutsatirani Iye ndi momwe amachitira. Ndiko kulondola.

15 Tsopano, ife tikhoza kuganizira, ngati inu mumapita kuchokera apa... Ngati ine ndimapita ku Chicago usikuuno, ine ndikhoza kupita panja ndi kukadzipezera kampasi, ndi kuti, "Tsopano tiyeni tiwone, Chicago ali mbali iyi. Chabwino, ine ndikhotera kumanja." Ine sindingatuluke mu Jeffersonville. Mukuona? Ine ndiyenera ndizipezere mapu a msewu wake. Ndipo pamakhala—pamakhala zoyalidwa... njira yomveka bwino kuti ndithe kupita ku Chicago pa ulendo wa maora sikisi kapena seveni oyenda pa galimoto, koma ine sindingakhoze kungodulira njira iliyonse. Ndege siingangodulira njira iliyonse; imakhala ndi—msewu wa ndege kapena utali winawake ndi zinthu zomwe iyo iyenera kuwulukira, madigiri enaake omwe iyo imayenera kukhalamo.

16 Pamakhala njira yopangidwiratu, ndipo Mulungu ali nayo njira. Mulungu ali nayo njira ya Mpingo Wake, ya anthu Ake. Ndipo Iye sanaikonze Iyo nkomwe kuti izilamuliridwa ndi mapapa, makardinolo, bishopu wamkulu, kapena oyang'anira akuluakulu. Mzimu Woyera ndiye Mphunzitsi wa Mpingo wa Mulungu wamoyo, kuti awukuze Iwo. Ndipo chiyero chonse sichimapita kwa kardinolo kapena wansembe, kuti zikamupange iye kukhala munthu woyera mu—mu mpingo, chirichonse. Anthu wamba amakhala chimodzimidzi basi... amakhala nawo ufulu wochulukanso kwa Mzimu Woyera monga mlaliki aliyense, m'busa, dikoni, trastii, china chirichonsecho. Anthu wamba!

17 Ndipo chifukwa chimene iwo amadzitchulira izo kuti Chiniko-lai... Monga ife tinali nazo izo usiku wathawu, Chinikolai, ife tinawaswa mawuwo ndipo tinawatenga iwo kuchokera ku Chigriki. Ndipo N-i-c-k-o, amathanthauza... *Nicko*, amene amathanthauza "kugonjetsa kapena kulanda." Chiyani? N-i-c-k-o, Chiniko-lai, *anthu wamba*. "Kugonjetsa anthu wamba," ndi kuwalanda powapatsa iwo kulamulira kwa amuna, azibusa oti aziwaphunzitsa iwo ndipo nkumakhala... nkumakhala ndi kugamula kwawo kwawo limodzi. Ndi momwe Nicene Council inachitikira. Chifukwa ambiri anakumana pamodzi ndipo anakonza zoti azichita mu Nicene Council. Ife sitiri... sitikufuna kuti tiyankhule zambiri pa zimenezo, chifukwa zimenezo ndi za Lachinayi usiku, ku Nicene Council.

18 Koma kumeneko ndi kumene Mpingo wa Roma Katolika unayambira, kuchokera mu gulu la anthu omwe anali owatembenuza a Paulo Woyera, ndi Ireniasi, ndi Marteni Woyera, kumapitirira mmusi. Iwo anali Akhristu otembenuka mtima akupita ku... amachoka ku chikunja amapita ku Chikhristu, koma ankafuna kuwukokera mpingo kubwerera mu kachitidwe ka Chipangano Chakale, monga kukhala ndi ansembe aakulu, ndi—ndi utumwi wolowezana, monga papa wina kwa papa wina, papa wina. Ngati tingakhoze kupitirira nazo kudutsa mu Baibulo ili, inu mungapeze kuti ndizo ndendende basi

zoonadi ndi mmene Mulungu anachitsutsira chinthucho kuyambira pachiyambi pomwe; ndipo m'badwo wa mpingo wa usiku wathawu, anati, "Ine ndimadana nacho icho!" ndipo chomwechonso Mpingo.

¹⁹ Mulungu sanakonze kuti Mpingo uziyendetsedwa ndi anthu. Mulungu amayendetsa Mpingo Wake, ndipo Iye amawuyendetsa iwo kudzera mu mphatso za Mzimu. Mphatso za Mzimu zimakhala mu Mpingo kuti zikawukonze mzimuwo. Ali nawo maudindo asanu otumikira mu Mpingo Wake. Woyamba wa iwo ndi atumwi, kapena, mamishonare. Mmishonare ndi maitanidwe apamwamba kwambiri amene alipo, mtumwi. Mawu akuti *mmishonare* amatanthauza "mmodzi wotumidwa"; *mtumwi* amatanthauza "mmodzi wotumidwa." Chifukwa chimene iwo anasankhira kumatchedwa amishonare, ine sindikudziwa. Koma iwo ndi atumwi. Chabwino. Atumwi, aneneri, aphunzitsi, alaliki, abusa. Tsopano, amenewo ndi maudindo ochita kusankhidwa a Mulungu kwa Mpingo Wake.

²⁰ Ndiye mu mpingo wamba uliwonse mumakhala mphatso naini zauzimu zimene zimabwera pakati pa anthu, zimenezo ndi, chidziwitso, nzeru, mphatso ya machiritso, kuchita kwa zozizwitsa, kuyankhula ndi malirime, kutanthauzira kwa malirime. Ndipo zinthu zonse izi zimapita mthupi wamba lililonse. Ndipo munthu aliyense mu mpingo amakhala ndi utumiki payekha, ndipo utumiki wayekha umenewo umayendera limodzi ndi utumiki wonsewo, kukamangiriza Thupi la Yesu Khristu. Ndipo palibepo. . .

²¹ Tsopano, kumbukirani izi, kuti apa pali. . . Ine ndijambula mizere imeneyi usikuuno. Mpingo woyamba, Efeso; Smurna, Pergamo, Tiyatira, Sarde, Filadelfiya, Laodikaya. Tsopano, kumbukirani pamene izi zikupitirira, mpingo *uwu* unali ndi chidzalo cha Mzimu, koma pamapeto pa m'badwo wa mpingo ife tikupeza kuti Iwo unali ukufinyidwira panja. M'badwo wotsatira wa mpingo unafinyira mopitirira pang'ono; mowonjeza pang'ono; mpaka *uwu* apa, panangotsala kachidutswa kakang'ono chabe. "Iwe uli nazo zinthu pang'ono," Iye anatero. Oh, pamene ife tidzafike ku M'badwo wa Mpingo wa Tiyatira umenewo!

²² Tsopano, umenewo utabwera, Mulungu anadzadzutsa wachi German dzina lake Martin Luther yemwe anadzawubwezeretsa Mpingo kachiwiri. Iwo unadzayamba mopitirira pang'ono, iye analalikira Kulungamitsidwa; motsatira kunadzabwera Martin Luther, anadalalikira Kulungamitsidwa. Potsatira kunadzabwera John Wesley ndipo anadalalikira Kuyetsedwa. Ndiye mu m'badwo wa mpingo *uwu* *apa*, iwo anabwereranso molunjika kubwerera ku Ubatizo wa Mzimu Woyera kachiwiri, ndi zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa, zikutsikira pansu pomwe. *Apa* ndi pomwe zinadzatulukira kudutsa zaka fifitini handiredi za Mibadwo ya Mdima. Ndipo kumeneko ndi kumene

wa mdima kwambiri...kapena ndi kumene tinakhala ndi nthawi yayitali kwambiri ya mpingo mu mibadwo ya mpingo. Ndiye *apa* ndi pamene zinayamba kumabwera chokwera, Kulungamitsidwa, Kuyeretsedwa, Ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo Baibulo linanena kuti, “Pamapeto a mbadwo *uno*, kuti ochepa apang’ono awa apa adzafinyidwira pansi chifukwa mpingo womwe uja wa Pentekoste udzayamba kumachita chinthu chomwe chomwecho chimene iwo anachiyamba mmbuyo *kuno*, Chinikolai.” (O Mulungu, ndiloleni ine nditseke pakamwa panga mpaka nditadzafika kwa zimenezo.) Inu mukuwona? Zimene ine ndikuwona kumeneko. Mwawona, mpaka inu mutawona apa. Ndipo ine ndikuwonetsani inu kuti mtumiki wa m’badwo wa mpingo uno adzadana nazo zipembedzo. Mzimu udzawuka mwa ana. Nthawizonse zakhala zikuchitika. Ndipo tsopano ife tiri ndi . . .

²³ Tsopano, ngati inu mungazindikire izi, momwe Iwo unali wopambana apa, unadzatuluka, ndipo potsiriza anadzawubanikitsa Iwo njira yonse mpaka kutuluka. Kenako Iwo ukuyambanso kubwerera. Luther anadzawukokera Iwo mmbuyo, Kulungamitsidwa; Kuyeretsedwa; Ubatizo wa Mzimu Woyera; ndiyeno pa nthawi yotsiriza kumene, iye akuwubanikitsa Iwo mpaka pansi, mpaka Uwu wangotsala pang’ono kuti utheretu, pangotsala apang’ono kwambiri chabe pamenepo, ndipo ndi pamene iye akukuwa akuti “Ngati Iye safupikitsa ntchitoyo chifukwa cha Osankhidwa, sipadzakhala mnofu uti udzapolumutsidwe.” Mukuona? Ndi zimenezotu, pa nthawi yotsiriza kumene. Tsopano muzikumbukira zimenezo.

²⁴ Tsopano ife tiyambira pa M’badwo wa Mpingo wa Smurna uwu. Poyamba ine ndikufuna kuti ndizigawegawe zimenezo apa pa pepala lina limene ine—limene ine ndiri nalo. Tsopano, m’badwo wa mpingo wachiwiri pokhala Smurna, ndipo ine ndikukhulupirira inu nonse mudzavomerezana nane (kapena ine ndikuyembekeza inu mukutero, kapena mwatheka, mulimonse) kuti Ireniasi anali nyenyezi ya m’badwo wa mpingo umenewo. Iye anali mtumiki wa Mulungu chifukwa iye anasesa dzikolo, anapita ku France (Gaul), kumusi kumeneko, ndipo iye anakhazikitsako mipingo, ndipo umodzi uliwonse wa iyo umakhazikitsidwa pa ubatizo wa Mzimu Woyera, kuyankhula mmalirime, kuwukitsa akufa, kuchiritsa odwala, kuletsa mvula, ndi kumachita zozizwitsa tsiku ndi tsiku. Iwo ankadziwa kuti Mulungu wamoyo ankakhala pakati pa anthu. Ameneyo anali munthu wa Mulungu, chifukwa Yesu anati, “Palibe munthu amene angathe kuchita...” Kapena, a—anthu anati, “Palibe munthu amene angachite ntchito izi pokhapokha Mulungu atakhala naye iye.” Uyo anali Nikodemo amene anamuwuzwa Yesu zimenezo.

²⁵ Tsopano, mzinda wazamalonda; malo ogulitsira aku Lydia ndi kumadzulo. Mzinda wachitatu mmakulidwe ku Asia, mzinda

waukulu wa doko. Wodziwika chifukwa cha chuma, makachisi, nyumba, masukulu, mankhwala ndi sayansi. Ayuda ankakhala ku—ku Smurna, ndipo iwo anawalalikira anthu a ku Smurna. Polekapu anali bishopu woyamba wa ku Smurna. Polekapu ndi antchito ena okhulupirika anakhazikitsa chikhulupiriro chakuya cha Mulungu mwa Asimurna okhulupirira. Azibambo oyambirira a mpingo anapereka chilimbikitso cha Choonadi kwa Smurna.

²⁶ M'badwo wa mpingo wa Smurna, dzina la mpingo linali Smurna, *Smurna*, kani, ilo limatanthauza “kuwawa,” mure. Zimalumikizana ndi akufa, chifukwa iwo amafa.

²⁷ Mpingo wozunzidwa, Mulungu ankawatcha iwo “ozunzidwa.” Mulungu amayang’ana pa kuzunzidwa kwawo, ndipo anapereka chisomo kuti apirire izo. Iye amayang’ana pa zisautso zake, ndipo anawapatsa iwo chigonjetso pa imfa. Amayang’ana pa umphawi wawo, ndipo anawapatsa iwo chuma mwa Iye. Mpingo wa Smurna unadutsa mu ng’ango ya moto ya masautso, koma, zinali fungo lonunkhira labwino kwa Iye. Ndiwo Otsalira aja tsopano, osati mpingo wonse wa Smurna; Otsalira okha ndi amene ine ndikuwanena. Masiku aakulu *teni a chisautso* akutanthauza “zaka teni za chizunzo cha magazi.”

²⁸ Ine sindikudziwa ngati ndingathe kutchula dzina limeneli, kapena kulitchula ilo, kapena ayi. Uyu anali mfumu panthawi imeneyo, ine ndikukhulupirira anali mmodzi wokhetsa magazi kwambiri kuposa mmodzi aliyense wa iwo kuyambira Nero mu 67, D-i-o-c-l-e-t-i-a-n. Mchaka cha 303 mpaka 312 A.D.

²⁹ Mulungu akumulimbikitsa Smurna kuti akhale wokhulupirika kufikira imfa, monga Iye anali, “Ndipo Ine ndidzakupatsa iwe korona wa Moyo, monga momwe Atate wandipatsira Ine.” Mulungu analonjeza wogonjetsayo (mmasautso) chigonjetso pa imfa yachiwiri, “Musawawope iwo omwe angaphe thupi, koma Iye amene angathe kuwononga solo, kapena, kupha solo.” Iwo . . . Anthu a ku Smurna anali oti apirire mpaka kumapeto, “Musawope anthunu, ndipo korona wa Moyo adzapatsidwa kwa inu.” Kuzunzidwa kwa Chikhristu mmibadwo kukuimiridwa mmibadwo ya mpingo, wa Smurna, ndi zofunikira kwambiri. Ife tifuna kuti tifike kwa izo pang’ono pokha, Ambuye akalola.

³⁰ Tsopano, ngati ena a inu mutaphonye zina za izi pamene . . . ngati ine ndikuzilemba izo mofulumirirapo pang’ono kwambiri kwa kalasi yonse, ndiye tidza . . . ndife . . . inu ndithudi mutha kudzazipeza izo kuchokera kwa ife nthawi iliyonse yomwe inu mungafune kutero, ife tidzakhala okondwera kutero kuti—kuti tidzakupatseni inu zimenezo. (Mundikhululukire ine.)

³¹ Tsopano pa mutu wa 2 ndi ndime ya 8, ife tikuyamba usikuuno. Tsopano, kodi ife tinamusiyira Iye pati usiku wathawu? Iye ndithudi anali . . . ankadana nacho Chinikolai

chimenecho. Nkulondola uko? Tsopano kodi Mulungu akuchita chiyani? Zimene timayenera kuti tizifufuze poyamba? Vumbulutso la Yesu Khristu, Yemwe Iye ali ndi chimene Iye ali. Tsopano chinthu chachikulu chotsatira, ife tikupeza kuti Iye amadana ndi chirichonse chomwe chingaike chirichonse kuti chizilamulira pa Mpingo Wake kupatula Iyemwini. Iye ndi Mulungu wa nsanje.

³² Momwe ine ndikufunira nditaima, chifukwa ife tangotsala ndi ndime zinayi zokha, kuti ndiwerenge mobwereza kanthu kena kakang'ono. Ndi angati angakumbukire nthawi imene mneneri wabwino, Samuele, pamene Israeli yense ankafuna kumakhala monga dziko lonse? Kodi inu mukukumbukira zimenezo? Ndipo mneneriyo anawawuza iwo, anati, "Inu mukulakwitsa!" Koma iwo ankafuna kuti azikhala monga Afilisti, ndi monga a—ena onse a iwo. Chabwino, ndizo ndendende zimene zinachitika mu m'badwo wa mpingo woyamba kumene uwu. Ndi zodabwitsa kuti anthu samafuna kuti Mulungu aziwatsogolera iwo. Iwo amafuna kuti azitsatira...iwo amafuna munthu winawake. Israeli, anapanga kulakwitsa kwakukulu kwambiri kuposa zonse zomwe anayamba azipangapo, pamene...Chisomo chinali chitawapatsa kale mneneri, mtsogoleri, chinawapatsa iwo mwanawankhosa monga chitetezero, ndipo chimawapatsa iwo chakudya kuchokera mmiyamba, ndi zinthu zabwino zonse zimene chisomo chinawapatsa iwo, ndipo komabe, mu Eksodo 19, iwo ankafuna lamulo. Iwo ankafuna kuti azipanga madokotala aumulungu, ndi kukhala nawo amuna ena, iwo ankafuna kuti azikhala ndi kanthu koti azichita mwa Iwo, nawonso.

³³ Munthu nthawizonse amayesetsa kuchenjera kuti amupose Mlengi kumene yemwe anamupanga iye, ndipo iye samachita chinthu koma kudzipha yekha. Monga ma Lamlungu angapo apitawo ine ndinalalikira pa—pa *Chipembedzo Chosakanizika*. Ndipo ndizo ndendende. Pamene inu musakaniza chirichonse, icho sichingakhoze konse...icho chimatha! Icho chathedwa, icho sichingabwererenso aponso. Mphongolo sangakhoze kudziberekanso konse ndi kudzakhala ndi mphongolo wina, chifukwa iye—iye ndi mphongolo, iye ndi wosakanizidwa. Chimanga chabwino, inu simungathe kukolola chimanga chabwino kuchokera ku chimanga chabwino cha haiburidi. Izo sizingatheke nkomwe...Icho chikhoza kumera, koma icho—icho, oh, icho sichimakhala chabwino nkomwe. Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Chirichonse chimene chiri chosakanizidwa si chabwino ayi.

³⁴ Ndipo chipembedzo chosakanizidwa sichabwino ayi! Bola ngati inu mukuyesera kuwonjezera chinachake kwa chimene Mulungu ananena, kapena kuchita chinachake chimene Mulungu sakufuna kuti inu muzichita, ndi chipembedzo

chosakanizika. Izo zikhoza kuwoneka zokongola. Oh, chimanga cha haiburidi chimawoneka chokongola kuposa chimanga chamakolo. Mphongolo yokalamba imagwira ntchito kuposa abulu awiri. Chabwino, ndizo...Izo si kugwira ntchito, m'bale, ndi chisomo chimene tinapulumsidwa nacho. "Ife sitimapulumutsidwa chifukwa cha zintchito, koma mwa chisomo." Chotero izo zikhoza...Ine ndikuyembekeza simukuganiza kuti zoyankhula izi...Inu—mwakhala mopanikizika, ndipo ine—ine ndikuzimverera izo pamwamba pano. Inu mukuona? Chifukwa pali Apresbateria, Amethodisti, ndi mitundu yonse mkati muno. Ife tikudziwa zimenezo. Ndipo chotero ine—ine ndikuzimverera izo. Ndipo inu muyenera mumasuke pang'ono inueni kwa kanthawi, muzipanga kudzigwedeza kuja, chomwecho.

³⁵ Tsopano, mvetserani. Chirichonse cha haiburidi sichabwino. Inu muyenera kutenga chapachiyambi, momwe Mulungu anachipangira icho, mukatero mukhala ndi chinachake chimene chiri chenicheni.

³⁶ Tsopano, ife tikupeza ndiye kuti mpingo uwu wa Israeli, pamene iwo ankapitirira chitsogolo, Mulungu anali atawadyetsa iwo, ndipo atawasamalira iwo, ndipo anawachitira iwo chirichonse. Ndipo potsiriza iwo anayang'ana kwa Afilisiti, ndi Aamori, ndi...ndi ena osiyanasiyana, ndipo anati, "Ife tikufuna mfumu! Iwo ali ndi chinachake chimene ife tiribe."

³⁷ Ndicho chinthu chomwecho chimene anthu akuchita lero. Ena a awa, alongo athu, amayang'ana pa televizioni ndi kumuwona Gloria Swanson, kapena aliyense amene iwo... ena a akazi amenewo atavala mtundu wina wa diresi, ndipo iwo sangakhoze basi kupirira izo mpaka iwo atapeza yawo. Mukuona? Mukamuwona mkazi wina mtawuni, "Oh, kodi izo si zabwino?" Inu muli nazo chiyani ndi zimene iye wavala? Anthu, ndi a choncho basi, ine ndinati ndi tsiku la—la kusanzirana, wina amafuna kumusanzira mzakeyo. Inu mutenge...Pali a Elvis Presley ambirimбири tsopano, ine—ine ndikukuuzani inu, inu simungathe kuwadzazitsa iwo mmagalimoto okhala ndi ngolo awo, chifukwa iye anakhala wotchuka mu zachithupithupi zosan-...zosanzira!

³⁸ Ife tiri ndi chinthu chomwe chomwecho mu chipembedzo. A...Ine ndimawerenga mbiriyakale ya Martin Luther, ndipo aliyense wa inu azambiriyakale mukudziwa. Iwo anati sichinali chinthu chachinsinsi kuti Luther anatsutsa mpingo wa Katolika ndipo nkumapitirira nazo izo, koma chinsinsi chachikulu kwambiri, chinali chakuti iye amakhoza kudzutsa mutu wake pamwamba pa zotentheka zonse zimene zinatsatira chitsitsimutso chake ndipo nkukhalabe ndi Mawu. Ndi chimene chinali chozizwitsa, momwe Mulungu anamusungira iye kukhala womvetsa zinthu ndi wosakhotakhota.

³⁹ Tsopano, chotero iwo anabwera kwa Samueli uyu. Iwo anati, “Utipangire ife do... kapena utipangire ife mfu—mfumu.” Ndipo Ambuye anamuuya iye kuti Iye wakana lingaliro limenelo, ndendende basi zomwe Iye anazikana kuno ndi bungwe.

⁴⁰ Chimodzimodzi basi monga Iye anazikanira izo, Iye amakana mabungwe. Iye samakana magulu, koma bungwe. Magulu, ife tiyenera kukhala nawo iwo. Koma bungwe ife sitikuyenera kukhala nalo, chifukwa ilo limalemba malire: “Ndife *Akuti-ndi-akuti*.” Kodi ndinu Mkhristu? “Ndine wa Methodisti.” Kodi ndinu Mkhristu? “Ndine wa Baptisti.” Zimenezo sizitanthauza kanthu kuposa nkumba mu khola. Izo ziribe kanthu kochita ndi Ichu, ayi nkomwe. Mkhristu!

⁴¹ Ine ndinamufunsa mtsikana usiku wina, pa nsanja, “Kodi ndiwe Mkhristu?”

Iye anati, “Bwanji, ine ndikupatsani inu kuti mumvetsetse, ine ndimayatsa kandulo usiku uliwonse.” Ngati kuti zimenezo zinali ndi chochita chirichonse ndi Chikhristu!

⁴² Bambo wina anati, “Chabwino, ndine wa Chimereka. Ndithudi!” Chabwino, zimenezo ziribe kanthu kochita ndi Ichu, palibepo kalikonse. Ndiwe Mkhristu chifukwa ndiwe wa Ufumu wina. Uko nkulondola. Ndipo ndiwe—iwe uli mu Ufumu wina, mmwamba.

⁴³ Tsopano, kodi Samuele anachita chiyani? Chinthu chomwe chomwecho chimene Mulungu anachita apa. Samuele anamuitanitsa Israeli pamodzi, iye anati, “Tsopano, mveterani kwa ine. Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Kodi inakhalapo nthawi imodzi pamene ine ndinakuwuzanipo inu chirichonse chimene sichinali choona?” Anati, “Ine—Ndine mneneri wa Mulungu pakati panu. Ndiuzeni ine nthawi imodzi yomwe ine ndinakuwuzanipo chirichonse mu Dzina la Ambuye chomwe sichinadzachitike.” Ndi zimene Samuele ananena kwa iwo. Iye anati, “Ndipo kodi Mulungu sanakudyetseni inu ndi kukusamalirani inu ndi kupanga zinthu zonsezi?” Anati, “Inu mukuchita tchimo poyesa kumachita monga mafuko enawo.”

“Oh . . .” iwo anati.

⁴⁴ Iye anati, “Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachakenso. Kodi ine ndinayamba ndatengapo ndalama iliyonse kwa inu? Kodi ine ndinayamba ndakupemphanipo chopereka? Kapena kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye chimene sichinadzachitike?”

Iwo anati, “Ayi. Inu simunatengepo ndalama zathu, izo nzoona. Ndipo inu simunatiuzepo ife kalikonse mu Dzina la Ambuye kamene sikanadzachitike.”

Iye anati, “Ndiye ndimvereni ine! Inu mukuchimwa poyesa kuchita monga ena onse a iwo.” Koma iwo ankafuna mfumu,

mulimonse! Mosalabadira kaya kuti zinali zolondola kapena zolakwika, iwo—iwo ankafuna kuchita lingaliro lawo.

⁴⁵ Ndicho chinthu chomwecho chimene mpingo unachita komwe kuno ku Efeso, iwo anatenga chiphunzitso cha Chinikolai. Ndipo pamene iwo anatero, izo zinawakankhira iwo mkati momwe kuti atembenuze chikunja ndi Chikhristu kukhala chimodzi ndipo zinayambitsa zaka fifitini handiredi za Mibadwo ya Mdimba. Ndipo pamene Luther anawachotsamo iwo, ngati (kuzungulira kwachiwiri) Achilutera sanachite chinthu chofanana ndi chimene iwo anachita mmbuyo ku Efeso! Ndendende.

⁴⁶ Tsopano, ngati inu mungazindikire, zoyikapo nyalizo sizinaikidwe mofanana monga *chomwecho*. Izo zinayamba chotsika mbali *iyi* ndipo nkumabwera chokwera. Chabwino, chokwera kwambiri chinali patali ndi kumene Iye amaima chinali ichi pamwamba *apa*. Ndipo Chikhristu chimazimirira pang'onopang'ono pamene chimachoka pamene Iye amaimirira mmawonekedwe a mtanda, monga ife tingamuwonere Iye mu mutu wa 4; mmawonekedwe a mtanda monga *chonchi*. Ndipo *ili* ndi dzanja Lake lamanja, *ilo* linali dzanja Lake lamanzere. Tsopano, pomwe *apa*, Iye anali ndi dzanja Lake pa mpingo *uwu* ndi pa mpingo *uwo*. Iye anali zonse Alpha ndi Omega ndipo, zoono, onse anali pakati pa ziwirizo, zilembo zina zonsezo. Koma motsindika Iye anati, “Alpha ndi Omega.” Iye anali ndi utawaleza pamutu Pake, chimene chinali pangano Lake.

⁴⁷ Tsopano, ngati inu mungazindikire, kuwala kwa Pentekoste, kumene iko kunayambira, pang'onopang'ono kunadzazimirira. Amuna awa, Ireniasi, Polekapu, ena onse a iwo amasindikiza umboni wawo ndi magazi awo, mpaka pomaliza zinafinyira Chikhristu mundima wawukulu wa masiku.

⁴⁸ Tsopano taonani, m'badwo woyamba mbali inayo ya mtumbira wawukulu, kubwera uko kunali Kuwala pang'ono, Kuwala kochuluka, kenako Kuwala kochuluka. Onani momwe Iko kunayambira kumawala kenanso, kumabwera ku tsiku limenelo. Ndipo tsopano kumapeto kwa m'badwo *uno*, zinanenedweratu apa kuti zidzafika ku *Laodikaya*, “wofunda.” Tsopano, ndi izi apa. Bwanji, ngati chinthu *ichi* apa chinawabweretsa iwo kwa *ichi*, ife tingafunirenji icho kuno mu Pentekoste?

⁴⁹ Ndipo inu mukudziwa Baibulo linati, “Padzakhala chirombo.” Ndipo ife tikudziwa kuti ndizo upapa wa Chiroma. Ndiko kulondola ndendende. Ndiyeno iwo akanadzapanga fano kwa chirombo chimenecho. Kodi fano ndi chiyani? Chinachake chopangidwa mofanana monga icho. Ndipo ndicho chitaganya cha mipingo, ndipo Pentekoste ili mmenemo. Idzafikapo nthawi yoti mwina mudzakhala wa bungwe kapena inu simudzatha kutsegula khomo lanu. Tsopano inu mukuwona ngati zimenezo

si zoon! Ndi chifukwa chake ife timazipuntha izo kuti zife. Inde, bwana. Inu simudzatha... Kutsika kuposa zimenezo, iwo adzayesetsa kuti akupanikizeni inu moyipa kwambiri, mpaka iwo atayesetsa kuti... sadzakulolani inu kuti muzigula kapena kugulitsa pokhapokha inu mutakhala ndi chilemba pa inu. Izo zikuzibweretsa izo mkati.

⁵⁰ Ndizo chimodzimidzi basi monga tsiku lijali, iwo ankawawotcha iwo, iwo... Ine ndinaima pamenepo mu bwalo limenero; ndinalira ngati khanda pamene ndimayang'ana kumtunda uko kumene omenya amakhala mu bwalo lakale ilo. Ndipo—ndi kuziwona zinthu zimenezo, ndikuziwa kuti ambiri a abale anga Achikristu anadyedwa ndi mikango ndipo—ndipo amang'ambidwa mzidutswa pabwalo kumeneko, ndipo akazi ndi ana aang'ono ndi zinthu. Ndipo ine ndikuganiza, ngati iwo onse ankapita mnthaka mwa chikhulupiriro, kodi ine ndiwalole apite mnthaka pano? Ayi, bwana, m'bale! Mulungu, ndiloleni ine ndiimire Chikhulupiriro chomwe chinaperekedwa kamodzi kwa oyera! Chinthu chomwe chija, ziribe kanthu ndi zosatchuka bwanji...

⁵¹ Winawake nthawizonse amafuna kunena, “Chabwino,...” Winawake ananena osati kale kwambiri... Oh! Ndi atumiki angati otchuka mmundamu andiimbira ine ndikuti, “M'bale Branham, ngati inu simusiya zimenezo, bungwe lirilonse lizitsutsana nanu inu.”

⁵² “Bwanji,” ine ndinati, “alipo Mmodzi yemwe satero, ndiye Mmodzi amene ali Kumwamba. Ndiye Mmodzi yemwe ine ndikumuyembekezera.” Mukuona? Tsopano, ine ndimawakonda anthu mu bungwe lirilonse. Ndithudi. Koma kodi ine ndinayamba ndakuwuzanipo inu chirichonse chimene Ambuye... mu Dzina la Ambuye, sichinadzachitike? Mukuona? Kodi chirichonse chimakhala chikunenedwa ndi kuchitidwa molondola? Kodi ine ndinayamba ndakupemphanipo inu ndalama? Ndiye mukhale kunjja kwa mabungwewo! Muzikhala amfulu mwa Khristu, muzilola Mzimu Woyera nthawizonse uziyenderera mkati ndi kunjja kwa mpingo.

⁵³ Chinthu chokhacho chofunikira, muchotse zosiyana maganizo pang'ono izi zikhale kutali ndi inu. Timalingaliro tating'ono, ndi kumverera kwachirendo pang'ono pozungulira inu za abale, ndi zinthu monga choncho, zisasenipo izo! Musalole muzu woyipidwa uliwonse ulowe konse mmojo mwanu. Ngati inu mutero, izo zidzakuwumitsani inu. Kulondola. Muzikhala ndi chikondi! Ine sindikusamala kuti anthu akukudani inu mochuluka bwanji, inu muziwakonda iwo mulimonse. Ngati inu simungachite zimenezo, inu mukusowa... a... inu simuli... inu simunasindikizidwe, inu mukadali ndi malo omasuka panobe. Chotero kazibwerani, mubwerere, ndipo pakasindikizidwe pamenepo bwino bwino ndi Magazi a Khristu.

Iwo adzakuyeretsani inu kuchoka ku mizu yonse yoyipidwa. Inde.

⁵⁴ Tsopano, onani, koma ife tikuyesetsanso. Mdalitso wa Pentekoste unagwa cha mu 1906, kwinakwake kumeneko. Pali mtumiki amene wakhala nafe usikuuno, mmishonare wochokera ku Tibet, mmodzi wa fi- . . . Ine sindikunena izi chifukwa iye ali pano; ine ndikudalira kuti sanapite kwawo. Ine ndikuganiza kuti iye akadali pano, anali woti atiyankhula ife pang’ono ine ndisanafike kuno. Ndipo munthu ameneyo amakumbukira koyamba kwa Pentekoste. Kunalibe bungwe lirilonse, aliynse amakhala ndi zinthu mofanana. Oh, ndi zophweka bwanji kutenga sitepe yolakwika pamenepo, ndi momwe zimawonekera zabwino kwa aluntha.

⁵⁵ Taonani, Israeli ankadziwa pang’ono pamene iwo anali atayima kunja uko pa gombe, akufuula . . . Tsopano, inu mukuti, “Chipembedzo cha mtundu uwu ndi chinachake chatsopano.” Bwanji, ndi chakale kwambiri chimene chiripo. Ndithudi. Ngakhale dziko lisanapangidwe nkomwe, iwo anali akufuula ndi kumatamanda Mulungu. Mulungu ananena chomwecho, anamfunsa Yobu, “Kodi iye anali kuti pamene—pamene nyenyezi zammawa zinkaimba pamodzi, ndipo ana a Mulungu ankafuula ndi chisangalalo.” Zimenezo zinkachitika dziko lisanalengedwe nkomwe.

⁵⁶ Koma tsopano tayang’anani pa Israeli, anali atawona zozizwitsa. Ndiyo Pentekoste yoyambirira; Israeli, Pentekoste ya tsiku limenelo. Tsopano iwo anali atabweretsedwa kuchokera ku Igupto, Mulungu anali atawadalitsa iwo, anawapatsa iwo mitundu yonse ya zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa, ndipo anawawombola iwo. Ndipo pamene iwo anaima pa gombe limenelo ndipo nakhala ndi msonkhano wa Chipentekoste . . . Iwo anatero! Tsopano mvetserani. Mose anayimba mu Mzimu, ndipo Miriamu anatenga nkhotcho ndipo anathamanga kutsika gombe, akumenya nkhotcho imeneyi, akuvina mu Mzimu; ndipo ana aakazi a Israeli anamutsatira iye, akuvina mu Mzimu. Ngati umenewo si msonkhano wa Chipentekoste, ine sindinawuwonepo umodzi. Iwo sanakhulupirire kuti—dziko lolonjzedwa linali zaka forte mtsogolo mwawo. Ilo linali pafupifupi mamailosi forte okha. Koma zinawatengera iwo zaka forte kuti amalize mailosi forte ndi chifukwa chakuti iwo anasankha chinthu cholakwika. Iwo anasankha kukhala ndi lamulo mmalo mololera Mzimu Woyera kuti uziwatsogolera iwo, Lawi la Moto linkawadutsitsa iwo ndipo linkawatsogolera iwo. Iwo ankafuna kuti akhale ndi chinachake choti azichita okha; iwo ankafuna kukhala ndi ansembe ena, ndi olemekezeka ena, ndi mbalume pang’ono zomwe iwo akanamakanganapo, mmalo momangopitirira ndi kuwulola Mzimu Woyera uziwatsogolera iwo. Iwo anali mu Mzimu; Mulungu anali atapereka chirichonse,

koma iwo ankafuna kuti akhale ndi chinachake choti azichita mu Icho.

⁵⁷ Chimodzimodzi ngati kusakanizanso kachiwiri. Isiyeni ng'ombe yokha. Musiyeni kavalo yekha. Chisiyeni chakudya chokha. Iwo... Sayansi imadzinenera, mu *Reader's Digest*, nkhani ya zimenezo, ngati iwo azipitiriza kumasakaniza zakudya, ndipo anthu nkumadya izo... Monga nkukhu, iwo ayitenga nkukhu yosauka imeneyo mpaka iyo ilibe mapiko kapena miyendo. Ndipo ngati iyo igona, iyo imadzigoneka yokha kuti ife, izo zimangokhala moyo kwa chaka. Ndipo minofu yake imakhala yofewa kwambiri moti simungathe kuyidya iyo nkomwe. Ndipo anthu akumadya izo, zikuwapotoza anthu. Uko nkulondola.

⁵⁸ Inu mukudziwa, kugonana amuna okha okha kwachulukana pafupifupi forte peresenti mu United States, chaka chapitacho. Ndipo kodi inu mumadziwa kuti sayansi imati akazi akumakula mmawepawa awo ndipo akumachepera mchiuno, ndipo amuna akumachepera mmawepawa awo ndipo akumakula mchiuno? Inu mukudya mbewu zopotozedwa, inu mukudya zinthu zopotozedwa. Thupi lanu linapangidwa kuti lizikula bwino ndi zinthu zachirengedwe. Ndipo izo zikuchita chiyani? Izo zikusintha ngakhale njira yachirengedwe ya amuna ndi akazi, mpaka Hollywood, ngakhale boma lathu, ndi chirichonse chadzaza ndi zopotoza. Kodi iye akuchita chiyani? Iwo akuzibweretsa izo pa iwookha ndi mtengo wawo wa chidziwitso, akudzipha okha.

⁵⁹ Bwererani kuchiyambi! Chisiyeni chokha chirengedwe. Musiyeni yekha Mulungu. Muwusunge Mpingo mu Mzimu Woyera; ndipo chokanicho kwa mabishopu onse awa ndi mapapa okhala ndi mitundu yonse ya chiphunzitso. Bwererani komwe ife tinayambirako. Mubwerere kumeneko. Yesu atabwera usikuuno, inu mungati, "Ndine wa Methodisti."

Iye angati, "Izo sizinali chomwecho kuyambira pachiyambi!"

"Ndine wa Presbateria."

"Izo sizinali chomwecho kuyambira pachiyambi!" Pachiyambi panali chiyani? Chokuchitikira cha pa Pentekoste cha ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndi momwe Iwo unayambira.

⁶⁰ Koma, onani, ife tinachita kuzipotola izo. Oh, zimapangitsa kukhala zokongola. Ndithudi. Mpingo wawung'ono umenewo ataima kuzungulira pamenepo akuvina, ndi kumafuula; ndi kumakayenda pa msewu, ndipo anthu kumaponyera miyala pa iwo, kumawaseka iwo, ndi chirichonse monga choncho. Zimenezo si zokongola kwambiri. "Koma tsopano ife tiri ndi Mayamiko aakulu, ndi Kachikhulupiriro ka Atumwi, ndipo, oh, Doctor Ph.D., L.L. awiri ma L.D., *Wakuti-ndi-wakuti* abusa athu." Ndi kumatulukako ndi kumati, "Ah-man," ngati mwana

wa ng'ombe yemwe akumva kupweteka, ndi kumapitirira nazo monga choncho, mtundu wonse wa zinthu zimenezo.

⁶¹ Ine ndikupepesa—ine sindimatanthauza kuti ndinene zimenezo. Mundikhululukire ine, ine sindimatanthauza kuti ndinene monga choncho. Mukuona? Ine sindimatanthauza zimenezo. Zimenezo ndi zosamuyenera wantchito wa Mulungu.

⁶² Koma, taonani, onsewo, ine...izo zinangobwera mmalingaliro anga, mwawona. Koma kuimirira ndi kunena zinthu zosiyanasiyana zonsezo monga choncho, kuphunzira pasanati...inu mukudziwa, nkuti, “Tsopano, ayi, sunanene bwino zimenezo. ‘Ah-man.’” Ine ndimakonda msonkhano wabwino, wachikale wa Chipentekoste kumene mphamvu ya Mulungu ikugwa, ndipo inu mumangokuwa ndi kumafuula ndi kumatamanda Mulungu, kumakhala ndi nthawi yopambana. Ndiyo njira yake; Mzimu utawagwira anthu. Koma ife...Inu simungamumve “Ameni!” nkomwe aponso, ndi “Ah-man.” Komabe, ndi pamene ife timapeza, inu mukuwona. Mabungwe awa ndi owuma, amanyada... .

⁶³ Tsopano anachita apo...Kodi unalipo ulosi wonena za zimenezo? Inu mukukumbukira ulosi wa Paulo usiku watha? “Ine ndikudziwa kuti nditachoka ine, mimbulu yolusa idzalowa pakati panu, ndipo amuna a gulu lanu lomwe, lanu... mu mpingo mwanu momwemo (Mpingo wa Roma Katolika umenewo, azidzabwera) adzauka pakati panu ndipo adzakokera ophunzira kuti awatsatire iwo.” Ndipo mimbulu ya Paulo, ife tikupeza, inadzakhala Achinikolai.

⁶⁴ Mvetserani pa Mzimu ukuyankhulanso kudzera mwa mneneri, “Mmasiku otsiriza zidzafika nthawi zowawitsa, chifukwa anthu adzakhala odzikonda okha, (‘Ndine Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti*, inu musandiuze ine za Iwo, tsopano. Ine ndikupatsani inu kuti mumvetse kuti ndine wa Presbateria. Aleluya!’ Kapena, ‘Ndine wa Pentekoste.’)” Kodi zimenezo zikupanga kusiyana kotani, ngati inu simuli wa Chipentekoste mwachirengedwe? Zokuchitikirani za izo, mwawona. Inde, bwana. “Ndine wa Assemblies.” “Ndine wa Mpingo wa Mulungu.” Chabwino zimenezo...kodi zimenezo zimapanga kusiyana kotani kwa Mulungu? Muyenera kukhala a Ufumu mmwamba kumeneko, mwawona. Uko nkulondola.

⁶⁵ Tsopano, ngati—ngati mukuwona, a...zinthu zonse izi zangokhala chipwirikiti cha—cha chisangalalo. Tsopano, Ilo linati, “Iwo akanadzakhala ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa kuposa kukonda Mulungu.” Oh, iwo sangapite ku tchalitchi Lamlungu usiku bola ngati pali purogalamu inayake yabwino pa televizioni. Oh, mai! Nthawizonse iwo...Ngakhale mipingo ili ndi magulu a mpira, ndi maphwando a msuzi, ndi maphwando a masewero, ndi, “okonda zokondweretsa koposa kukonda Mulungu, okuswa

pangano, onenera amzawo zoipa, osakhoza kudziletsa, ndi onyoza iwo amene ali abwino.” *Awa* kumawanyoza *iwo*, mwawona. *Awa* kumawanyoza *awo*, kumawatsamwitsa iwo. Onyoza iwo omwe *ali* abwino.

⁶⁶ Oh, inu mukuti, “Iwo ndi Achikominisi, m'bale.” Oh, ayi. Ayi, ayi.

⁶⁷ “Ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu, okuswa pangano, onenera amzawo zoipa, osakhoza kudziletsa, onyoza iwo omwe ali abwino, okhala nawo *mawonekedwe*. . .” Zochitika zachipembedzo, mwawona. “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yake.”

⁶⁸ Kodi inu mungakhale chiyani mu tsiku lino? Onani, “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu.” Kumapita ku tchalitchi mwauzimu basi monga mmene mungakhalire, Lamlungu, ndipo kumavala akabudula Lamlungu masana, kumatchetcha pabwalo ndi kumamwa panja wa Oertel's 92. Ndipo abusa amatuluka panja ndi kukasuta ndudu ndi kubwereranso, inu mukudziwa. “Kukhala nawo mawonekedwe aumulungu!”

⁶⁹ “Chabwino, abusa, iwo ali ndi tchalitchi kumtunda uko, iwo amandiuza ine kuti dona anachiritsidwa tsiku lina ku khan-. . .”

“Hmm. Hmm. Zamkhutu! Masiku a zozizwitsa anapita.”

⁷⁰ “Chabwino, inu mukudziwa chiyani? Ine—ine—ine ndinapita uko ku tchalitchi chaching'ono usiku wina, mishoni yaying'ono ija uko pakona, ndipo kumeneko kunali winawake amaimirira pamwamba apo, amayankhula chinachake, chibwi-. . .”

“Oh, wokonedwa, usadzayende konse ndi zonga zimenezo. Amenewo ndi agalu openga. Mai! Iwe usadzapusitsike nazo zimenezo. Amenewo ndi oyera-odzigidubuza. Inu musadzati nkomwe. . .”

⁷¹ “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu ndipo nkumakana mphamvu yake, kwa oterowo chokaniko. Pakuti awa ndi amene amayenda nyumba ndi nyumba natsogolera akazi opusa otengeka ndi zilakolako zosiyanasiyana, osakhoza konse kuphonzira kapena kufika ku chidziwitso cha Choonadi.” Ndizo ndependende kulondola. Ndi zimenezotu, gulu la chithandizo la azimayi, gulu *ili*, *ilo*. Mpingo wosauka uli ndi magulu ambirimbiri mwakuti ukulepheranso kulalikira Uthenga. Abusa sangakhale nawo koma maminiti twente, ndipo ayenera kulankhula za chinachake pamenepo. Mukuona? Ngati satero, gulu la madikoni likumana nawo iwo. Inde, bwana.

⁷² Oh, m'bale, kodi m'busa wabwino amayenera kuchita chiyani lero? Angochita mwakukhoza mmene iye angathere kuima pamenepo ndi kudula miyendoyo pamene ikufunikira kutero, ndi kulola zidutswa zigwere pomwe izo zingafunikire;

ndi kuponyera izo kunja uko. Ndizo zonse. Inde, bwana. Uko nkulondola. Osati—osamulekerera aliyense, kungolalikira Mawu ndi kukhala nawo Iwo molondola, kumangowakhomerera iwo. Ngati akuponyerani inu mu ndende, kawalalikireni Iwo mu ndende. Ngati akakuikani kwina kulikonseko, kalalikireni kulikonse kumene inu mungapiteko; kazingomapitirirani nazo, kumalalikira. Ndiko kulondola. Tsopano, ndi zomwe zachitika. Mwawona, iwo akuzibanikitsa izo.

⁷³ Tsopano tikubwera ku—ku M’badwo wa Smurna. Ndime ya 8:

. . . kwa mngelo wa mpingo wa Smurna lemba; Zinthu izi anena woyamba ndi wotsiriza, amene anali wakufa ndipo ali ndi moyo;

⁷⁴ Ine ndikufuna kuti inu muzindikire nthawi iliyonse yomwe Iye akudziwonetsera Yekha ku m’badwo wa mpingo, Iye amapereka chinachake cha Umulungu Wake. Ndicho chinthu choyamba chimene Iye amayesetsa kuti achidziwitse kwa mpingo, kuti, ndicho Umulungu Wake. Iye ndi Mulungu! Inu mukuwona nkhani yaikulu kumbuyo kuno yomwe Ireniasi ndi iwo ankakanganirana? Iwo ankayesera kumanena kuti Mulungu mu kuwala kwa dziko kutatu, ndipo ndi Mulungu mwa anthu atatu, ndi Mulungu mwa *ichi*. Iye anati, “Kulibeko chinthu choterocho! Ndi maudindo a Munthu mmodzi, ndipo ameneyo ndi Mulungu Wamphamvuzonse.” Uko nkulondola. Chotero inu musatero. . . iwo amakhala nazo izo nthawizonse. Ndipo Mulungu apa pachiyambi akudziwonetsera Yekha cha chimodzi cha Wake—cha Maumulungu Ake. Inu mukuwona Iye akudziwonetsera Yekha, poyamba apa, “Ine ndine Iye amene anali, amene alipo, ndi amene adzabwera. Ndipo Ndine Wamphamvuzonse.” Apa Iye akuyamba ndi M’badwo wa Smurna tsopano.

⁷⁵ Tsopano mvetserani kwa Iye, “Ine. . .”

. . . kwa mngelo wa mpingo wa Smurna. . . (Ndipo ife tikukhulupirira kuti ameneyo ndi Ireniasi.) . . . lemba; Zinthu izi anena woyamba ndi wotsiriza, . . .

Mukuona? Anadziwonetsera Yekha, “Ndine Mulungu, tsopano, wa m’badwo wa mpingo uno. Ine sindikufuna milungu inai kapena isanu yosiyanasiyana kuno. Ine—Ndine Mulungu. Mwaona, ndizimenezotu.”

. . . amene anali wakufa, ndipo ndi wamoyo; (Ameni!)

⁷⁶ Tsopano, amenewo ndi—ndi malonje. Tsopano—tsopano Smurna amatanthauza “kuwawa,” ndipo amachokera ku mawu akuti mure—mure. Ndipo mpi—mpingo woyamba—mpingo woyamba, ndi. . . unali utataya chikondi chake choyamba, mpingo wa Efeso. Ndipo mpingo uwu unayamba kukhala nawo “muzu wa kuwawa” umabwera mwa iwo chifukwa chakuti mpingo uwu, mpingo waukulu, gawo lalikulu (ambiri

a iwo, nthawizonse) amakhomerera motsutsana ndi Mzimu Woyera kuti ukulamulira mu mpingo, ndipo iwo ankafuna kuti azidzilamulira, iwoeni. Iwo ankafuna kukhazikitsa unsembe, iwo ankafuna kuti azichita monga anthu a Chipangano Chakale ankachitira. Iwo ankafuna unsembe. Ndipo iwo... Ngati milungu yachikunja, kumbuyo uko, kumene iwo anatembenuzidwako, iwo anali ndi ansembe ndi ena otero a... a Jupiter, ndi ansembe aku Venus, ndi ena otero; iwo—iwo—iwo ankafuna kuti abweretsemo mwa iwo chinthu chomwe chomwecho kuti awapange amuna *awa*. Mwaona, chinthu chonsecho ndi chachikunja kuyamba ndi kuyamba. Achikunja onse amakhala nawo ansembe amenewo ndi zinthu zonga zimenezo. Koma—koma Mpingo wa Mulungu wamoyo, ndi zachirendo kwa iwowo. Khristu ndiye Wansembe wathu, Wansembe wathu Wamkulu. Ife tiri naye Wansembe Wamkulu, gome nalonso limene ife timadyerapo.

⁷⁷ Tsopano, mpingo uwu unayamba kuphukira “muzu wa kuwawa.” Chifukwa chiyani? Iwo unkaipidwa ndi iwo amene amafuna kuti azipitirira ndi Mzimu Woyera. Chikondi chinali chitazirala, ndipo iwo anali kuyesera kusinthanitsa icho ndi tizikhulupiriro ndi zipembedzo, amachoka ku utsogoleri wa Mzimu Woyera. Taganizani za zimenezo! Ndi chifukwa chake ku—ku—kuwawa kunali mwa iwo. Chabwino.

⁷⁸ Tsopano, mpingo woyamba, uwu...kuwawa kunayamba kukwawiramo. Mpingo wachiwiri, kunawonjezekera pang'ono. Ndipo, potsiriza, iko kunakwawira mkati chifukwa iwo anali “kupanga mpingo wabwinoko”; iwo ankaganiza kuti akutero. Pomwe apa iwo anali ndi chinachake cholemekezeka, anthu opambana Achiroma amakhoza kubweramo. Chifukwa chiyani? Iwo anali ndi papa, iwo anali ndi—iwo anali ndi amuna otchuka, makardinolo, ndi zina zotero. Iwo amavala bwino. Iwo anali atachokako ku phokoso lonse ndi chirichonse zimene iwo anali nazo; amangokhala chete. Kuwonetsera kuti iwo amafa. Uh-nhu. Uh-nhu. Iwo amafa. Ndipo chotero iwo anakhala olemekezeka ndipo anapanga thupi labwinoko. Chinthu choyambirira pamwamba apa, iwo anali nacho chinthu chonsecho mu chipembedzo chachikulu chachipembedzo, tchalitchi cha Chiroma cha Padziko lonse, Mpingo wa Roma Katolika mu M'badwo wa Mdimba. Chabwino, atatero, iwo anakhala ndi olemekezeka, ndipo iwo anali ndi kalasi.

⁷⁹ Oh, izo zinali zokongola kwambiri kuposa momwe iwo anakakonda kumaima panja pa msewu, “ndipo amayenda mu zikopa za nkhosa ngati zikopa za mbuzi, ndi osowa, ndipo amachekedwa pakati, ndi—ndi kumasekedwa, ndipo amanyozedwa,” ndipo monga Paulo ananenera mu Ahebri mutu wa 11.

⁸⁰ Bwanji, tchalitchi chopambana, chachikulu ichi, chovala mwinjiro wabwino, ndi zovala zamkati, ndi—ndi zinthu zina

zonse izi zomwe iwo amavala monga choncho. Ndithudi, izo zimawoneka zolemekezeka, “Abambo, M’busa, Dokotala, Abambo *Akuti-ndi-akuti*.” Oh, mai! Amakhoza kuvala zenizeni “galu,” pamenepo.

⁸¹ Koma, inu mukuwona, icho chinali chinthu cha haiburidi. Haiburidi! Mwaona, icho chinalibe Moyo uliwonse mwa icho. Ndipo iwo sangabwereranso mmbuyo aponso, ndi chifukwa chake iwo sanawukeponso. Chitsitsimutso cha Achilutera sichinadzawukenso kachiwiri. Chitsitsimutso cha Wesley sichinadzawukenso kachiwiri. Chitsitsimutso cha Nazarene sichinadzawukenso. Komanso chitsitsimutso cha Pentekoste sichidzawukanso. Chifukwa chiyani? Chifukwa inu munachipha icho. Inu munachipanga haiburidi icho ndi dziko, ndi lingaliro la Chinikolai, osalola Mzimu Woyera kukhala nayo njira Yake. Uko nkulondola. Inu mwachipanga tchalitchi haiburidi, ndipo icho chikulephera kuti chidzibale chokha kachiwiri. Pamene inu muberekananso, inu mumakhala ndi Amethodisti ambiri; Abaptisti akaberekananso, amakhala ndi Abaptisti ambiri; Akatolika akaberekananso, amakhala ndi Akatolika ochuluka; amakhala ndi chinthu chomwecho chimene inu mukuchichotsa ku khutu. Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake; pamene Mzimu Woyera ubwereranso, Iwo ukubweretsa kubadwa *kwatsopano* ndi Moyo *watsopano*; kutembenuka. Ubatizo wa Mzimu; umawubwezeretsanso Mpingo kwa iwo wokha kachiwiri, umabwezeretsanso Moyo mmenemo.

⁸² Chimanga cha haiburidi sichimakhala ndi moyo mwa ichocho. Moyo wake ndi uti, watsala pang’ono kutayika. Tsopano, ife tikuzipeza zimenezo mu M’badwo wa Mdimu umenewo, “Chaching’ono chimene uli nacho, ugwiritsitse kwa icho,” Iye anatero. Iwo anali atazifinyira panja izo. Tsopano, koma izo sizidzibalanso zokha kenanso. Tsopano, a . . .

⁸³ Koma Thupi la Yesu Khristu si—si bungwe ayi. Thupi la Yesu Khristu ndi Thupi lachinsinsi, ndi Thupi la . . . mu Ufumu umene uli Ufumu wauzimu womwe unakhazikitsidwa padziko lapansi ndi Yesu Khristu kukhala Mfumu ya Ufumu umenewu, Wansembe Wamkulu kukapereka nsembe za apaulendo mu Ufumu umenewu. Iye ndi Mneneri (Mawu) amene amalalikira Choonadi ndi kubweretsa Kuwala kwa Mulungu mu Ufumu umenewu; ndipo Iye ali zonse Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu, mu Ufumu uwu. Ndipo kodi ife timalowamo chotani mu Ufumu umenewu? mwa chipembedzo? mwa chikalata? pogwirana chanza? Koma “mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi” ndiro Thupi lachinsinsi la Yesu Khristu, ndipo ife timabatizidwira mmenemo, osati mwa madzi, osati mwa kukonkha, osati mwa kutsanulira, osati mwa mtundu uliwonse wa ubatizo wa mmadzi, koma “mwa Mzimu umodzi, Mzimu Woyera, ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi

limodzi,” Akorinto Woyamba 12. Inde, ife timabatizidwira kulowa mu Thupi ili mwa Mzimu umodzi, Mzimu Woyera, ndiye kuti sitiri a kalikonse koma Khristu. Ndinu a Khristu. Ndi Ufumu wachinsinsi wa Mulungu umene wakhazikitsidwa, kuti ife timabwera mwa Iwo mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Ine ndimazikonda Zimenezo! Hmm!

Kuli anthu pafupi kulikonse,
 Amene mitima yawo yonse ikuyaka
 Ndi Moto umene unagwa pa Pentekoste,
 Umene unawatsuka ndi kuwapanga iwo
 kuyera;
 Oh, Iwo ukutentha tsopano mkati mwa mtima
 wanga,
 Oh, ulemelero kwa Dzina Lake!
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wawo.

Ndine mmodzi wawo, ndine mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti
 ndine mmodzi wawo; (Aleluya!)
 Mmodzi wawo, ndine mmodzi wawo,
 Tsopano ndine wokondwa kuti ndikhoza
 kunena ndine mmodzi wawo.

Ngakhale anthu awa ali osaphunzira, (D.D.D.
 Ph.D. Mwawona). . . akhoza kukhala
 osaphunzira,
 Kapena obwekerera za kutchuka kwa mdziko,
 Onse analandira Pentekoste yawo,
 Kubatizidwa mu Dzina la Yesu;
 Ndipo akunena tsopano, mtali mtali,
 Mphamvu Yake ndi yomweyo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wawo.

Kodi sindinu okondwa? Inde, bwana. Mmodzi wawo basi. Ndizo zonse.

⁸⁴ Ine ndikukumbukira ndikuyenda kudutsa ku Memphis, dona wamng’ono uja, wachikulire wachikuda uja, mutu wake utatsamira pamenepo. Iye anati, “Mmawa wabwino, abusa.”

Ine ndinati, “Kodi inu mwadziwa bwanji kuti ine ndi m’busa?”

Iye anati, “Ambuye andiuzwa ine, ‘M’busa wake akubwera mu msewu, akhala atavala chipewa cha bulauni, atanyamula sutikesi.” Anati, “Ine ndinadziwa kuti inu munali iye pamene ine ndinakuwonani inu mukubwera.” Mukuona? Oh, iye anali mmodzi wawo. Uko nkulondola! Oh, momwe Mulungu aliri wabwino!

⁸⁵ Tsopano ine ndikukhulupirira chinachake. . . [M’bale Branham akuwerenga kakalata kamene wapatsidwa—Mkonzi].

“Mtsikana wamng’ono yemwe munamupempherera—la, Lamlungu usiku, wochokera ku Bedford, akuyenera kuti wamwalira kumene. Izi sizingakhale... Chonde mukhale ndi pemphero.” Mtsikana wamng’ono yemwe ife... iwo anamupempherera kuno Lamlungu usiku, wochokera ku Bedford, “wango—wangomwalira kumene,” iwo akutero. Tiyeni tikhale ndi pemphero:

⁸⁶ Ambuye Yesu, ine ndikupemphera kuti mwanjira ina, mwanjira ina, Ambuye, mulole mapemphero athu apite akafike kwa mwana ameneyo. Ife tikukapereka kanthu kakang’onoko kwa Inu, Atate wathu Mulungu. Ndipo ife tikuganiza za anthu amenewo omwe anali pano ndipo anapemphera ndi kufunsa pemphero la mtsikana wamng’ono uyo. O Atate Mulungu, ine ndikupempha kuti—kuti lipoti ili lisakhale chomwecho, Atate; ife sitikudziwa, koma ine ndikupemphera kuti Inu mutichitire chifundo ndipo mutipatse mphamvu ndipo mulole kanthu kakang’onoko kadzutsidwe ndi kukakhala moyo kwa ulemelero wa Mulungu. Mu Dzina la Yesu Khristu ife tikupempha izi. Amen. Ambuye Yesu awonjezere madalitso Ake.

⁸⁷ Tsopano, mpingo. Tsopano, dzina la mpingo limalumikizana ndi khalidwe lake. Kodi inu munazindikira tanthauzo la *Smurna* “kuwawa”? Ndipo inu mukuzindikira umodzi uliwonse wa mpingo tsopano, ndi dzina la mpingo liri ndi chochita ndi khalidwe la mpingo. Ine ndikhoza kunena chinachake apa; koma ine kulibwino ndisatero, chifukwa inu mukhoza kundimva ine molakwika. Mukuona?

⁸⁸ Dzina lanu limatero, nalonso. Inu mwina simukudziwa zimenezo, koma ilo limatero. Oh, inde. Inu mukuti tsopano, “Ndi manambala.” Ayi, sichoncho. Pamene Yakobo anabadwa iwo anamutcha iye *Yakobo* chimene chiri “wolanda;” koma pamene iye anadzalimbana ndi Mngelo, Mulungu anadzamusintha dzina lake kukhala *Israeli*, “kalonga.” Nkulondola uko? Saulo anali “Saulo wa ku Tariso,” munthu wankhanza; koma, pamene iye anabwera kwa Yesu, iye anadzatchedwa “Paulo.” Dzina la Simoni linali “Simoni”; koma pamene iye anabwera kwa Yesu, iye anamutcha *Petro*, “mwala wawung’ono.” Oh, inde, bwana. Dzi... Dzina lanu limayenderana ndi zomwe muli... Ilo limakhudzana ndi khalidwe lanu.

⁸⁹ Ndipo mpingo uwu unkatchedwa *Smurna* chifukwa chakuti iwo umafa. *Smurna* amatanthauza “kuwawa.” Mwakuyankhula kwina, muzu wa kuwawidwa unali kutulukira ndipo unali kutsamwitsa izo, unali panjira yake kupita ku mure. Ndi chimene iwo amadzozera nacho matupi, mure, mwaona. Anali mure, lubani, ngati mafuta onunkhiritsa. Mure amagwiritsidwa ntchito po—podzozera matupi akufa iwo akatha kuwakonza iwo, ndi zina zotero. Zimayanjana ndi imfa, ndipo mpingo unali ukufa.

⁹⁰ Ndipo, oh, kodi inu simukuwona, lero, abwenzi, kusuntha kwakukulu kwa Chipentekoste komwe kunali ndi Moyo zaka zingapo zapitazo, inu simukuwona kuti iwo ukudzozedwa tsopano ndi mure? Mukuona? Mafuta omwewo omwe anali mu mpingo uno *apa* abwera pansu ndikudzadzozo uwu kumusi *kuno*; akufa chifukwa akubwerera ku nsanza zachipembedzo, ndipo akuvula mwinjiro wawo woyera, oyera. Anthu apang'ono omwe anayima kunja uko, ndi Mzimu Woyera weniweni, anayankhula ndi malirime, ndipo anawonetsera Mulungu. Ndipo, m'bale, iwo anali owona mtima ndipo, "onse awubweya ndi kukula kwa bwalo lonselo." Iwo—iwo mwamtheradi anali enieni, mukanakhoza kuwadalira iwo konsekonse. Tsopano inu simukudziwa choti muchidalire komanso woti mumudalire. Mukuona? Pali chinachake chimene chinachitika. Chinachake chinachitika. Ndi chiyani? Iwo akudzozedwa ndi mure, wa kuwawa. Kudzuka. Chimodzi. . .

⁹¹ Nchiyani chinayambitsa izo? Mmodzi anadzalowa mkati, panali—mpingo wotchedwa, woyamba, unali General Council. Kenako iwo anadzawutcha iwo Assemblies of God. Kuchokera ku Assemblies of God kunadzabwera Church of God. Kuchokera ku Church of God, ndiye iwo anayamba kuyang'ana kutsidya, kuti, "Ndinu Assemblies." Ena amati, "Ndinu Church of God." Ndiye kuchokera pamenepo kunadzabwera United Pentecostal Church of God, pa nkhanayo. Ndiyeno, chinthu choyamba inu mukudziwa, mmalo movomereza Kuwala ndi kuyenda Mmenemo, bwanji, iwo anali atadzipanga okha bungwe mpaka iwo samakhoza kulandira Kuwala.

⁹² Tsopano, pamene—ubatizo mu Dzina la "Yesu Khristu" unabweretsedwa mmalo mwa "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera" kupita kwa Assemblies of God, iwo anali atadzimangirira okha kale kotero iwo sakanakhoza kusintha izo. Ndipo iwo amadziwa kuti Icho ndi Choonadi! Ine ndikutsutsa aliyense wa iwo kuti asonyeze kuti Izo sizikugwirizana ndi Baibulo. Izo ndi mwamtheradi Choonadi. Koma kodi iwo angachite chiyani? Iwo sangachite zimenezo. Mwawona, iwo akhoza kuphwanya kachikhulupiriro kawo, iwo sangatero.

⁹³ Ndiye Aumodzi anachita chiani? Mmalo movomereza Icho ndi kumapitirira nazo, iwo anakhuthala: "Mulungu adalitsike kwanthawizonse! Ife tiri nako Kuwala, ndipo inu mulibe. Ndife. . ." Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anazipanga izo bungwe. Inu simungathe kumupanga bungwe Mulungu. Mulungu alibe nkomwe mawonekedwe, Baibulo linatero. Ayi, palibe zamwambo ndi Mulungu.

⁹⁴ Tsopano, ndiye a Assemblies anayesera kuti amupange bungwe Iye ndi kuwapanga iwo...awo...awo a—a—Mpingo weniweni. Ndipo kenako Aumodzi anadzabwerapo, anadzayesera kupanga bungwe wawo, ndipo iwo "anali ndi Kuwala kochuluka." Chotero kodi iwo achita chiyani? Iwo

anazithawitsa izo ndi kudzikonda kwawo, njira zowawa zomwe iwo anayendetsera izo. Mmallo moperekera izo ndi mchere komanso kukoma, iwo anayesera kumuchotsa pachiyanjano winayo, kukhala wopanda chochita ndi iye. Ndipo ndi zomwe izo zinachita. Iwo anali atasesa, pamenepo. Chinthu choyamba inu mukudziwa, apo panadza china, iwo anali nazo *izi*, ndipo tsopano iwo anasiyana. Mmodzi anati, “Akubwera pa kavalo woyera.” Winayo anati, “Iye akubwera pamtambo woyera.” Mulungu adalitsike, ine ndiyambitsa bungwe kuno.” Mukuwona momwe iwo amachitira? Anafalitsa mure—mure. Kodi izo zinachita chiyani? Izo zinatsekereza ubale.

⁹⁵ Akazi ambiri, amuna, usikuuno, mu Assemblies of God, akufuna atabwera ndi kudzabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, podziwa kuti Ndicho Choonadi cha Mulungu. Iwo angachotsedwe ngati iwo atatero.

⁹⁶ Ndipo ambiri a Umodzi a...Tsopano, sindine Waumodzi. Ine sindikhulupirira mu “umodzi” momwe iwo amachitira. Ine sindikhulupirira mwa *Yesu* monga iwo amanenera, “*Yesu*”; alipo a *Yesu* ambiri. Ndi *Ambuye Yesu Khristu*. Uko nkulondola. Tsopano, ndipo ine sinditero...Ine ndimakhulupirira zimenezo mosiyana ndi momwe iwo amachitira. Iwo amabatiza mu Dzina la Yesu, mu Dzina la Yesu kuti asinthike, kuti “Pobatzidwa (kusinthika) zimabweretsa Khristu kwa iwe ukabatizidwa mmadzi.” Ine sindimakhulupirira zimenezo. Ine ndimakhulupirira kuti kusinthika kumabwera ndi Magazi a Yesu Khristu kudzera mwa Mzimu Woyera. Uko nkulondola. Ubatizo ndi chochitika cha kunjira kokha kwa ntchito ya mkati yakusinthika imene yachitika. Mukuona? Chotero, ine sindimagwirizana nazo zimenezo. Nzabwino zimenezo, koma iwo onse ndi abale anga.

⁹⁷ Pamene ine ndinayamba monga mlaliki wa Baptisti, iwo anabwera pafupi ndikudzati, “M’bale Branham, inu mubwere kuno, ife—ife—ife tiri nawo Iwo ndipo ife tinawubweretsa Iwo kuno.”

⁹⁸ Ine ndinati, “Palibe mmodzi wa inu, ine ndimaima pakati pa magulu awiriwo ndikuti, ‘Ndife abale!’” Sindisamala za chiyani, ine sindisamala kaya munthu sakugwirizana nazo, izo sizipanga kachidutswa kamodzi kosiyanana ndi ine, iye akadali m’bale wanga.

⁹⁹ Ine ndiri naye m’bale yemwe amakonda chitumbuwa cha apulo; ine ndimakonda cha nthudza kwambiri, koma ine sindimuchotsa iye pachiyanjano. Iye akhoza kumadya chitumbuwa cha apulo chakecho ndipo ine ndizidya chitumbuwa changa cha nthudza. Ndipo ndimayika *nsuzi wa ng’ombe* pamwamba pa changa, ngati iye sakufuna icho, bwanji, iye akhoza kukhala nacho. Inu mukudziwa zimenezo...Ndi chiyani izo? Zinthu zopaka zimene iwo amaika pamenepo,

inu mukudziwa, “kirimu wopaka.” Ine ndimazikonda izo. Ndikukalamba kwambiri tsopano kuti ndingadye izo, koma ndizo. . . . Koma ine—ine—ine. . . . Ndizo zimene ine ndimazikonda. Ngati iye sazikonda izo, iye sayenera kuti adye izo. Izo ziri bwino, ine ndidya zanga. Koma iye akadali m'bale wanga apabe! Uko nkulondola.

100 Ndipo chotero ine—ine ndimazikonda zimenezo, ine ndimakonda chiyanjano. Koma pamene ife tilemberana malire monga chonchi, ndikuti, “Ayi, ichi ndi chipembedzo *chathu*,” ndipo osatha kukafikako ndi kukagwirana chanza ndi munthu winayo, ndi kuti, “Mulungu akudalitse, m'bale!” Mai! Ndi pamene inu mumazitchula chiyanjano. Ngati inu simungatero, inu muli ndi muzu wakuipidwa umenewo chimodzimodzi basi monga momwe a Smurna anali nawo mmbuyo uko, ndipo inu muyambitsa chinthu chomwe chomwecho. Chabwino, chotero dzina lawo linali “owawa.”

101 Achinikolai anapitirizabe kuwapondereza iwo mpaka Mibadwo ya Mdimba. M'badwo wa Luther unabweretsa sitepe yoyamba ya chisomo, Kuwala pang'ono kunayamba kuwala. Kenako kunadzabwera zitachitika zimenezo, kunadzabwera John Wesley ndi kuyeretsewa, anakula mowala pang'ono. Ndipo kenako kunadzabwera ubatizo wa Mzimu Woyera ndi Achipentekoste, kubwezeretsanso chikhulupiriro cha makolo. Koma iwo sakanatha kuzisunga izo mwanjira imeneyo, chotero iwo anazipanga izo bungwe, ndipo kenako iwo anayambanso kubwerera kupita mu Chinikolai kachiwiri. Ndendende basi zimene Baibulo linati iwo akanati adzachite.

102 Tsopano, ine ndiyenera ndipenye apa kapena ine ndizipeza izo. . . . ndatengapo nthawi yochulukirapo. Tiyeni tifike ku ndime ya 2, kapena. . . . imeneyo ingakhale ya 8, ndime ya 9. Chabwino, tsopano kuzunzidwa, ndime ya 9:

Ine ndikudziwa ntchito zako, masautso ako, . . . umphawi, (koma ndiwe wolemera) . . . (Oh, mai!) . . . Ine . . . (Tsopano Iye akuyankhula kwa Mpingo tsopano, Mpingo weniweni, osati enawo; iwo ankadana nazo ntchito izo za Chinikolai.) . . . Ine ndikudziwa mwano wa iwo omwe amadzinenera kuti ali Ayuda, ndipo siali, komatu ndiwo sunagoge wa Satana.

103 Tsopano, iwo amadandaula. Anali atakanthidwa ndi umphawi. A . . . Iwo anali atatenga zonse zimene iwo anali nazo. Iwo anali atamanga mpingo wawo wawung'ono monga chonchi, ndipo pokhala kuti iwo anali kagulu kakang'ono kwambiri, iwo anali atawakankhira iwo kunja, tchalitchi chachikulu chinali, chitangowafafanizapo iwo. Ndipo Iwo unati, “Ine ndikudziwa. Ine ndikudziwa kuti inu mukuchita kumasonkhana pa kangodya, inu mukumasonkhana mu ngalande, kapena kulikonseko kumene mungathe.” (Ndipo ine ndinafikamo mu

mphanga za manda mmene iwo amakomana; amapita pansi pa nthaka ndi kukakomana, ndi zinthu kumeneko.) “Ine ndikudziwa masautso anu, ndipo Ine ndikudziwa mavuto anu, ndi zina zotero monga choncho, koma inu mukupangidwa kukhala olemera kupyolera mmasautso amenewo.” Oh, mai! Ndiuzeni ine nthawi iliyonse imene chizunzo chikabwera pa Mpingo, icho chimawulimbikitsa Iwo. Nthawizonse icho chimawulimbikitsa Mpingo, mmasautso. “Ine ndikudziwa masautso ako, koma ndiwe wolemera.” Chifukwa chiyani? “Iwe wagwiritsitsa kwa Ine; ndiwe wolemera. Koma masautso ako sakukupweteka iwe.”

104 Tsopano, a...Kodi inu munazindikira? Achinikolai anali atadzipezera okha sunagoge tsopano. Baibulo linanena chomwecho apa. Kodi inu munazindikira izo apa mu ndime ya 9?

Kuti . . . amene . . . siali, koma ali sunagoge wa Satana.

105 Uh-nhu, Mpingo woona unali utakankhidwira panja. Achinikolai anali atalanda, ndipo a...anali atawathamangitsira panja anthu omwe anali ndi Mzimu Woyera, chotero momwemo iwo—iwo analibe nawo ntchito iwo. Ngati Smurna, mu Asia, akanangodziwa kokha kuti zinthuzo . . . kuti akorona a ofera akanawadikirira iwo, iwo akanadzidzimuka. Mukuona? Tsopano, mwa kuyankhula kwina, chiyani . . . pamene ulosi uwu unalembedwa ndipo unatumizidwa kumeneko, ndipo mpingo unazigwira izo, ndipo iwo anawona kuti anali iwowo amene anali kupita kukavala korona wa ofera, bwanji, iwo akanatero . . . bwanji, izo zikanawawopsyeza iwo pafupi kufa. Iwo anali akuyembekezera zimenezo nthawi iliyonse. Sanabwere mu m’badwo wawo. Ndiye mwinamwake ena a iwo anati, “Chabwino, inu mukudziwa—inukudziwa, ine ndikukuuzani inu, mneneri ameneyo amalakwitsa. Yohane amalakwitsa, iye—iye . . . chifukwa sizinatichitikire ife kuno mu Smurna.” Bwanji, izo zinali zoti zidzakhala zaka mazana mtsogolo. Mukuona? Koma pamene Mulungu ayankhula chirichonse, icho chimayenera kuti chidzachitike.

106 Apo ndi pamene ife timamiza chikhulupiriro chathu, pomwepo apo pa Mawu a Mulungu. Mulungu amasunga lonjezo lirilonse. Ziribe kanthu . . . Inu mukhoza kuganiza kuti ziyenera kuchitika pomwe pano, koma mwinamwake imeneyo sindiyo nthawi ya Mulungu kuti zichitike. “Koma Mawu Anga sadzabwerera kwa Ine opanda kanthu, koma Iwo adzakwaniritsa chimene Iwo anapangidwira.” Mulungu nthawizonse adzalemekeza Mawu Ake, ndipo mu nthawi Yake Yomwe yabwino Iwo adzakolola.

107 Chotero anthu awa anali amenewo, mpingo woyamba, koma mu mpingo umenewo munali khalidwe limene likanadzatulukira

mu mpingo wa Smurna mtsogolo. Tsopano, ndiye iwo anali oti adzavala korona wa ofera, ambiri a iwo anali oti adzaphedwa.

108 Tsopano tiyeni titenge ndi—ndime ya 10, pamene ife tikuwerenga izi:

Usawope chirichonse cha zinthu izi (sunagoge wa Satana) zimene iwe udzamva kuwawa: taona, mdierekezi adzakuponyera... iwe mndende, kuti iwe ukayesedwe; ndipo iwe udzakhala nacho chisautso masiku khumi: khala wokhulupirika kufikira imfa, ndipo Ine ndidzakupatsa iwe korona wa moyo.

109 Oh, mai! Iwo anauzidwa kuti asachite mantha pamene iwo ayitanidwa kuti akafere chawo—chipembedzo chawo. Tsopano, Mlongo Wood, kulikonse kumene inu muli, ine ndikuyembekeza kuti izi zikuthandizani inu. Mlongo Wood amandiuza ine, tsiku lina, iye samatha konse kumvetsetsa chifukwa chimene ena amatha kupulumutsidwa ndipo ena iyi. Nthawizina iwe umayenera kudziwa... Mulungu anawawuza anthu awa, “Tsopano, iwe usachite mantha za izo, chifukwa Satana adzakuponyera iwe mmenemo, chifukwa chakuti chovala cha Chinikolai ichi chimene chabwera ndipo chikukukankhirani inu mkati, chifukwa ine ndikulolani kuti inu mufere chifukwa cha Changa. Koma ine ndidzakupatsani inu korona wa Moyo tsiku limenelo.” Chotero musati... .

110 Tsopano penyani, Iye anati... Tsopano, ngati inu mungazindikire pamene ife tikuwerenga ndime ya 10 iyi. Ndiroleni ine ndiwerengenso iyo kachiwiri:

Usawope chirichonse cha zinthu izi zomwe udzamve kuwawa: taona, mdierekezi adzaponjera ena a inu mnyumba yandende, kuti mukayesedwe; ndipo inu mudzakhala nacho chisautso masiku khumi: koma khalani okhulupirika kwa... (Kodi inu munazindikira kuti sikuti mpaka? Sikuti mpaka imfa, koma “kufikira” imfa. Inu mukumvetsa zimenezo?) ... khalani okhulupirika kufikira imfa,... (Mukuona? Ndipo iwo anatero.)

111 Tsopano Iye anati, Satana... Kodi inu munazindikira amene Iye—amene Iye anamuika monga amene anali kuchita izo? Tsopano, *sunagoge wa Satana* uyu anali “Chinikolai.” Ife tikudziwa zimenezo. Si choncho izo? Ndiye linali bungwe, unsembe umene umakwera umene ukanadzawapangitsa anthu awa kuti azunzike, zomwe zikanadzawapangitsa anthu awa kuzunzika, ndipo iwo amayenera kukhala okhulupirika ku Uthenga *kufikira* imfa. Kodi inu munazindikira mu mwambo wa chikwati? osati *mpaka* imfa itatilekanitsa, koma “kufikira imfa ife timalekana.” Mukuona? Tsopano, *kufikira* ndi *mpaka* ndi zosiyana. Tsopano, iwo anali oti akhale okhulupirika kwa Khristu kufikira imfa. “Mupite mpaka kukafika ku imfa nazo

izo. Musachite mantha, chifukwa ine ndidzakupatsani inu korona.”

112 Tsopano awa “masiku khumi” omwe akuwakamba apa, masiku khumi. Tsiku mu Baibulo limaimira chaka. Ndipo *masiku khumi* anali a “zaka khumi” zotsiriza za ulamuliro wa D-i-o-c-l-e-a-t-i-o-n, Diocletian. Diocletian. Diocletian, imeneyo inali mfumu yayikulu ija yomwe inalamulira kumapeto...Chabwino, alipo mafumu angapo amene analamulira mu M’badwo wa Mpingo wa Efeso. Ndipo Nero, ine ndikukhulupirira, anali mmodzi. Ndipo Diocletian uyu apa anali womaliza yemwe analamulira, mu zaka khumi zotsiriza, ndipo iye anali wokhetsa magazi kwambiri wa iwo onse. Iye anangotenga mbali ndi gulu ili ndipo iwo—iwo anawazinga Akhristu, ndi kuwapha iwo, iwo anawawotcha iwo, iwo—iwo anachita chirichonse, ndipo izo zinali zaka khumi za chizunzo chamagazi kwambiri. Ndipo nthawi yake ndi ulamuliro wake zinali kuyambira 302 mpaka 312. Izo zinathetsa M’badwo wa Smurna, ndi kubwerapo kwa Konstantini. Ndipo iye anadzabwera mu 312, Konstantini anatero. Amenewo anali masiku khumi a masautso. Ndipo izo zinayambira ndi Nero ndipo zinadzathera ndi Diocletian. Ndipo izo zinayambira ndi Nero, zinali pafupifupi A.D. 64 pamene Nero anatenga mpando wachifumu.

113 Tsopano, ndime ya 11 ndi lonjezo. Tsopano ife tikhala ndi iyi tisanatseke:

*Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene
Mzimu akunena kwa mipingo; Iye amene alakika
sadzapwetekedwa ndi imfa yachiwiri.*

114 Tsopano, ine ndiyenera kuti ndinene chinachake apa, icho mwa dongosolo...Ngati ine ndikuganiza izo, mtima wanga, ndipo osazinena izo, ndiye kuti ndine wachinyengo. Mukuona? Ine ndikufuna inu kuti muzindikire chinachake apa mu Lemba ili, ndipo ine ndikuganiza kuti chinali chimodzi cha ziphiphiritso zazikulu kwambiri kwa ine kwa nthawi yayitali mpaka nditadziwa. Tsopano tiyeni tiwerenge zimenezo mwatcheru kwenikweni, tsopano. Mukuona?

*Iye amene ali nalo khutu (Mwa kuyankhula kwina,
“ali nalo khutu kuti amve”; mwaona, ndizo “tsegulani
kwa Mzimu.”) muloleni iye amve chimene Mzimu
akunena kwa mipingo; . . .*

Tsopano onani, chinthu chomwe chomwechi, kuzunzidwa uku ndi zonse zimabwera. Gawo lirilonse la izo limakamalizira mu mpingo uliwonse. *Mipingo.*

*. . .Mzimu anena kwa mipingo; Iye amene
adzagonjetsa. . . (Mu mpingo uti? Wa Efeso? Inde.
Chabwino. Smurna? Inde, yonse ya iyo.) . . .Iye amene*

adzagonjetsa mmipingo yonse *sadzapwetekedwa ndi imfa yachiwiri.*

115 Iye amene ali mu mpingo wa Laodikaya amene adzagonjetsa chiyani? Adzagonjetsa Chinikolai, adzagonjetsa zinthu za mdziko lapansi, adzagonjetsa zipembedzo izi, adzagonjetsa za unsembe izi, adzagonjetsa chirichonse cha mdziko lapansi ndipo nagulitsa, ndi kumakonda Khristu. Inu simudzapwetekedwa ndi imfa yachiwiri. Chifukwa chiyani? Iye ali nawo Moyo Wamuyaya. Moyo Wamuyaya sungakhoze kufa. Yesu anati, "Iye amene amva kwa Ine ali nawo Moyo Wamuyaya, sadzafa konse. Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomaliza."

116 Tsopano, tsopano, pamenepo. . . Tsopano, inu muchita. . . Padzakhala ambiri omwe sadzagwirizana nazo izi, koma ine ndikufuna kuti inu muganizire mozama kwenikweni musanapange chigamulo chanu. Mukuona? Ine ndinena chinachake tsopano:

117 Ndi chifukwa chake ine sindimakhulupirira kuti alipo gehena Wamuyaya. Sipangakhale gehena Wamuyaya. Chifukwa ngati panakhalapo gehena Wamuyaya, ndiye kuti nthawizonse analipo gehena Wamuyaya, chifukwa Chamuyaya. . . Alipo mawonekedwe amodzi okha a Moyo Wamuyaya, ndipo ndi chimene ife tonse tikumenyanirana. Ndipo ngati inu muti mukapsye moto kwanthawizonse ndi kwa Muiyaya, ndiye kuti muyenera kudzakhala ndi Moyo Wamuyaya ukuyaka, ndiyeno adzakhala Mulungu akuyaka. Inu simungakhale ndi gehena Wamuyaya, ndipo Baibulo limanena momveka bwino kuti "gehena anachita kulengedwa." Ndipo ngati anachita kulengedwa, si Wamuyaya. Chirichonse chimene chiri Chamuyaya sichinalengedwe nkomwe; iye nthawizonse analipo, ndipo ndi Wamuyaya. Ndipo Baibulo limanena kuti "Gehena anapangidwira mdierekezi ndi angelo ake." Gehena analengedwa, iye si Wamuyaya. Ndipo ine sindimakhulupirira kuti munthu adzalangidwa Kwamuyaya.

118 Ine ndimakhulupirira kuti Baibulo limanena momveka bwino apa, kuti, "Iye amene alakika sadzapwetekedwa ndi imfa yachiwiri." Tsopano "imfa." Mawu akuti *imfa* amachokera ku. . . ndi ichi, ndi "kulekana." Tsopano, pamene ife tilekanitsidwa ndi Mulungu, mu tchimo, ife tafa kale; Baibulo limanena chomwecho. Ife timatalikirana ndi Mulungu, ife timadulidwa, ndife akufa mu tchimo ndi zolakwa; ndife alendo kwa Mulungu komanso kwa chuma Chake. Ndiyeno pamene ife tamulandira Mulungu ndi kukhala nawo Moyo Wamuyaya, ife timakhala ana Ake ndi gawo la Iye.

119 Mwana wanga wamwamuna wamng'ono apo, Joseph, ali gawo la ine, ziribe kanthu zomwe ine. . . iye angachite konse. Iye. . . Ine ndikhoza. . . Iye mwina akhoza kusakhala. . . Ngati ine ndikadakhala munthu wolemera kwambiri ndipo nkukhala

ndi cholowa chambiri, iye akhoza, iye akhoza ngakhale kulandira chirichonse; komabe iye ndi mwana wamwamuna, iye ndi gawo la ine. Ndithudi, iye ndi gawo la ine. Tsopano, ine sindingathe konse kumukana iye monga ine sindingathe kudzikana ndekha, chifukwa iye ndi gawo la ine. Kuyeza kwa magazi kukhoza kuwonetsera kuti iye ndi wanga. Mukuona?

¹²⁰ Ndipo kuyeza kwa Magazi kumawonetsa ngati iwe uli wa Mulungu kapena ayi. Mukuona? Ndinu ana a Mulungu ndipo muli nawo Moyo Wamuyaya. Koma moyo umene uchimwa, *moyo* umenewo udzalekanitsidwa. Nkulondola uko? Ndiye iwo sudzakhalaponso. Tsopano taonani. Chirichonse chimene chinali ndi chiyambi chimakhala ndi mathero, chifukwa chirichonse chimene chinali ndi chiyambi ndi chirengedwe. Koma Mulungu sanalengedwe, Iye anali Mulungu nthawi zonse. Palibe malo amene Iye analengedwa. Ndipo njira yokhayo imene ife tingakhalire nawo Moyo Wamuyaya ndi kukhala gawo la chirengedwe chimenecho. Ulemelero! Oh, ngati ife tingakhoze kuwuwona Iwo! Mukuwona zomwe Mzimu Woyera umakuchitirani inu? Ndi Mzimu Woyera, Mlengi Mwiniwake, Mulungu Atate mmawonekedwe a Mzimu, wotchedwa “Mzimu Woyera” chifukwa Iwo unali pa thupi lotchedwa Yesu, Mwana Wake; kuti Iye anamlenga Yesu, thupilo, ndi chifukwa chake Ilo limayenera kufa. Mulungu anadzakhala mu mnofu waumunthu uwu, ndipo khungu la magazi linasweka, ndipo Moyo wochokera mu khungu la magazi unadzabwereranso.

¹²¹ Ndipo ndi chifukwa chake wopembedza wakale mu Chipangano Chakale samachokapo... iye amachokapo ndi kutsutsika komweko kumene iye anali nako pamene amabwera. Koma mu Chipangano Chatsopano, Ahebri ananena, kuti, “Wopembedza akatsukidwa kamodzi sakhalanso ndi chikumbumtima cha tchimo.”

¹²² Tsopano, Chipangano Chakale; iwo ankabweretsa mwanawankhosa, iye ankamugoneka iye pansu, amayika manja ake pa iye, wopembedzayo; wansembe ankamudula pakhosi, iye ankamverera kuwukha magazi, ndipo amamva kuphupha kwa iye. Ndipo iye amafa, ndipo iye ankamverera thupi lake laling’ono likuwuma, ndipo iye amafa. Iye ankadziwa kuti izo zikanayenera kukhala iyeyo; mwanawankhosa amatenga malo ake. Wansembe amatenga magaziwo, amakawaika iwo paguwa ndipo—ndipo utsi unkakwera mmwamba, ndipo ilo limakhala pemphero la chikhululukiro kwa wop-... [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . ndipo moyo wa chinyama umenewo sumakhoza kubwerera pa munthu nkudzagwirizana ndi mzimu wa munthu, chifukwa ndi mzimu wa chinyama. Moyo wa chinyama ndi moyo wamunthu, iwo sukanakhoza kuchita zimenezo. Koma pamene a... Ndi chifukwa chake iye amachokapo ndi chikhumbo chomwecho kuti akachimwe, chinthu chomwe chomwecho. Amabwera chifukwa chochita

chigololo, ndipo amapereka nsembe yake, ndipo amabwereranso ali ndi chinthu chomwecho mmalingaliro mwake. Uko nkulondola.

¹²³ Koma apa pamene wopembedza... Oh, Mpingo wa Mulungu, musalephere kumvetsa izi! Wopembedzayo, akayenda kamodzi moonadi kupita kwa Mwana wa Mulungu ndipo mwa chikhulupiriro nkukakasanjika manja ake pa Iye (Oh, mai!), kuyang'ana apo mu nkhope Yake ali ndi malovu amenewo akuyenderera pa nkhope Yake, Magazi akuyenderera kumatsika pa nkhope Yake, nkunverera zowawa za “Mulungu Wanga! Mulungu Wanga! Chifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?” Oh, m'bale, pamene inu muwona mtengo wake umene unakuferani inu, ndi Yemwe Iye anali, Emanuele, Mulungu akufa mmalo mwanu.

¹²⁴ Ndiye chimachitika ndi chiyani? Wopembedza ndiye, pamene khungu la Magazi lija linasweka mwa Mwana wa Mulungu... Nchiyani chinapanga khungu la magazi limenelo?

¹²⁵ Ndinu chiyani? Ndinu kakhungu kamodzi kakang'ono kochokera kwa abambo anu. Chachikazi sichimakhala ndi magazi amoyo. Cha—chachikazi chimangobala dzira lokha; chofungatira, iye amayenera kuti anyamule—a—awutamire. Koma magazi amachokera kwa chachimuna, ndi chifukwa chake—mwana amatenga dzina la abambo ake. Ndiyeno, koma, mkazi akamakwatiwa kwa mwamuna, amatenga dzina lake, pa chifukwa cha ana; iye amadzakhala chofungatira cha mwana amene iye ati adzamuberekere mwamunayo. Koma monga ine ndinanenera: nkhuu itha kuyikira dzira, koma ngati iyo sinakhale limodzi ndi mbalame yamphongoyo, iyo siingaswe.

¹²⁶ Ndicho, ine ndinati, ndi chifukwa chake ife tiri ndi mipingo yambiri yakale, yozizira, yofunda lero. Iwo anatengera lingaliro la Chinikolai ili, ali ndi mulu wa zisa zodzaza ndi mazira ovunda, ndipo iwo sadzaswa nkomwe chifukwa alibe... Inu mukhoza kuchita chirichonse kwa iwo (kuwatcha iwo mabishopu, madikoni, ndi chirichonse), iwo sadzakhulupirira konse mu zizindikiro zowatsatira okhulupirira, chifukwa iwo sanakhalepo ndi Mwamunayo, Yesu Khristu. Ngati inu mungadzapatsidwe konse chonde ndi Mwamuna ameneyo wa mphamvu ya Mulungu...

¹²⁷ Pamene khungu la Magazi lija linaswedwa pamenepo pa Kalvare, ndipo Moyo uwo umene unali mmenemo, Yehova wachinyamata... Oh, izo ziyenera kukhala zokhudza!

¹²⁸ Inu mukudziwa, aliyense akufunafuna chizindikiro. Si choncho iwo? Aliyense akuti, “Oh, ndiwonetseni ine chizindikiro.” Myuda anati, “Ndiwonetseni ine chizindikiro.”

¹²⁹ Ndiroleni ine ndikupatseni inu chizindikiro. Mulungu anakupatsani inu chizindikiro nthawi ina. Iwo anafunsa chizindikiro. Israeli anafunsa chizindikiro. Iye anamuza

mneneri, “Ine ndidzawapatsa iwo chizindikiro chosatha: namwali adzaima. Namwali adzaima ndipo adzabala Mwana wamwamuna.” (Ameni.) “Iye adzatchedwa *Emanueli*, ‘Mulungu nafe.’” Chizindikiro chachikulu chomwe chinaperekedwapo.

¹³⁰ Pamene Mulungu, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, anapanga zowunikira za mmwamba. Mudzaima uko pa Phiri la Palomar ndipo mudzayang’ane kudutsa malo amenewo kutsidya, ndipo inu mutha kudzawona zaka handiredi ndi twente miliyoni za malo a kuwala. Mudzaziswe zimenezo mu mamailosi, ndi kuwoloka kumeneko kukadali mwezi, ndi nyenyezi, ndi maiko, ndipo Iye anazipanga zonsezo. Anangoziwuzira izo kuchokera mmanja Mwake, monga *choncho*. Inde!

¹³¹ Ndipo Mlengi wamkulu uja anadzakhala Mpulumutsi wanga. Anadzabwera mpaka ku khungu laling’ono la Magazi, osati kudzera mwa mwamuna, koma anabwera namwali kwa mkazi; ndipo anadzatenga mungu wawung’ono uwu kuchokera kwa mkazi, ndipo anadzadzipangira Yekha nyumba yaying’ono nakhala mmenemo. Oh, izo—izo—zikuyenera kukhala zokhudza! Yehova! Yehova, pa mulu wa manyowa mu khola, akulira. Yehova, ali modyeramo ziweto mwa mapesi. Chimenecho chinali chizindikiro chosatha, ena a anthu a mutu waukulu awa! Yehova, Mulungu, Mwana wolira (Aleluya!) mu khola lonunkha. Ndiyeno ife timaganiza kuti ndife winawake, kudzutsa mphuno yanu mmwamba; kuti ivumbe mvula, ingakumizeni inu; ndiyeno nkumayenda kumaganiza kuti ndinu winawake. Ndipo Yehova atagona modyera ng’ombe, pamwamba pa—pa mulu wa manyowa, akulira ngati wamng’ono...mwana wamng’ono aliyense. Izo ziyenera kukhala zokhudza! Ndicho chizindikiro. Mulungu anati, “Ine ndidzakupatsani inu chizindikiro chosatha.” Chimenecho ndicho chizindikiro chenicheni. Yehova, akusewera ngati mwana. Yehova! Yehova, akugwira ntchito mopalira matabwa, kumadula matabwa ngati kalipentala. Aleluya! Mai, oh, mai! Yehova, akusambitsa mapazi a asodzi. “Ine ndidzakupatsani inu chizindikiro.”

¹³² “Oh, koma ife tiyenera kukhala ndi abusa, inu mukudziwa, wokhala ndi mwinjiro ndi zingwe zonse, makolala, ndi...” Mukuona? Oh!

¹³³ “Ine ndidzakupatsani inu chizindikiro chosatha.” Yehova, ataimirira mmabwalo a milandu ali ndi malovu pa nkhope Yake. Yehova, atadzitambasula wamaliseche, mu thupi, pakati pa miyamba ndi dziko lapansi. Iye ananyoza manyazi a mtanda. Ife tiri nacho chifanizo Chake pamenepo ali ndi ka sanza kakang’ono kataphimbidwa pa Iye; zoonza zake ndi zakuti ndi wosema amene anachita zimenezo. Iwo anamuvula Iye maliseche, anamuchititsa Iye manyazi! Oh, gulu lija la achinyengo pamene ora limenelo linafika! Lino ndi tsiku la munthu, tsiku la Ambuye likubwera. Yehova! Yehova, akufa,

inde, palibe chomwe chinachitika. Yehova, akupemphera, palibe chomwe chinachitika. Hmm. Uko nkulondola. Izo ziyenera kukhala zokhudza! Icho ndi chizindikiro chosatha. Ndicho chizindikiro chimene amuna onse amayenera kuchidziwa. Kenako Iye anafa, Yehova anafa. Zitatero dziko linayamba kugwedezeka. Oh, mai!

¹³⁴ Kenako Iye anadzuka kuchokera mmanda ndipo anakwera Mmwamba. Yehova, kubwerera mmawonekedwe a Mzimu Woyera kuti adzakhale mu Mpingo Wake, pakati pa anthu Ake. Ulemelero! Yehova, kumayenda yenda mu mpingo, kumazindikira malingaliro a mmalingaliro. Yehova, kumachiritsa odwala. Yehova, kumayankhula kupyolera mu milomo mpaka munthuyo kulephera kuti adzilamulire yekha. Yehova, kubwereranso mu Chingerezi ndi kudzamasulira izo. Inu mukufuna chizindikiro? Ameni! Yehova ameneyo anadzabwera kwa wachiwerewere, anamudzutsa iye, komwe iye anali kwambiri—iye anali wotsikitsitsa kwambiri mpaka agalu samamuyang'ana iye, ndipo anamutsuka iye anayera ngati chipale ndipo anamupatsa iye mtima wangwiro ngati kakombo. Oh, mai! Yehova, kuchitenga chidakhwa chitagonera pamenepo mu ngalande ndipo ntchentche zikuwuluka pakamwa pakeponse, ndi kumupangitsa iye kulalikira Uthenga...?... Magazi a Yesu Khristu akutiyeretsa ife!

¹³⁵ Pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anapita ku mzinda wotsikitsitsa umene unalipo, ndi kwa anthu otsikitsitsa amene analipo, ndipo iwo anamupatsa Iye dzina lotsikitsitsa lomwe linalipo. Uko nkulondola. Iwo anamuchitira Iye choyipisitsa, ndipo ankamutcha Iye dzina loyipitsitsa lomwe likanakhocha kutchulidwa, “Bezebule,” mdierekezi. Lotsikitsitsa limene iwo akanakhocha kumupatsa Iye, munthu anamupatsa Iye.

¹³⁶ Koma Mulungu anamukweza Iye, ndipo Iye anamupatsa Iye Mpando wachifumu wapamwamba kwambiri mpaka Iye amayenera kuyang'ana pansu kuti awone Kumwamba. Ameni! Ulemelero! Ndipo anamupatsa Iye Dzina loposa maina onse omwe amatchulidwa Kumwamba ndi padziko lapansi, ndipo banja lonse Kumwamba ndi padziko lapansi lapatsidwa dzina la Iye. Ndicho chimene munthu ankaganiza za Iye; ndi chimene Mulungu ankaganiza za Iye. O Mulungu, mulole malingaliro anga akhale monga Anu, Atate. Inde, bwana. O Dzina lofunika!

¹³⁷ Tsopano, “Iye amene akhulupirira pa Ine ali nawo Moyo Wamuyaya.” Tsopano, ngati ulipo mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo inu mwawupeza iwo ndipo ife tikuwufunafuna iwo kudzera mwa Yesu Khristu, umenewo ndi Moyo wa Mulungu. Ndi pamene khungu la Magazi ilo linaswedwa pa Mwana wa Mulungu, ndipo Yehova wamng'ono uja yemwe anatsekeredwa mkati mwa Munthu uyu wotchedwa Yesu (pamene mwa Iye munkakhala chidzalo cha Umulungu mthupi), ndipo tsopano pamene ife tivomereza Magazi *amenewo*

kukhala chikhululukiro cha machimo athu, Mzimu uwo umene sunali pa munthu, koma pa Mulungu... Ulemelero! Baibulo linati, “Mwazi wa Mulungu.”

¹³⁸ Winawake anati, “Inu mukukumbukira, Iye... Musamanene chirichonse cha Ayuda, chifukwa Iye anali Myuda.” Iye sanali Myuda. Iye sanali Myuda kapena Wamitundu, Iye anali Mulungu. Uko nkulondola. Iye anali Magazi olengedwa. Mulungu anachipanga icho kukhala chapadera. Iye anali Ake Omwe, ndipo kupyolera mu Magazi olengedwa amenewo ife timawalandira Iwo ngati chikhululukiro chatu chifukwa Iye anafa imfa mmalo mwathu. Khungu la Magazi limenelo linadzasweka, linadzamasula Mzimu Woyera umenewo kuti udzabwerere pa ife, ndipo tsopano ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu kudzera mu kubadwa kwa Mzimu. Ndiye Moyo umene unali wa Mulungu, umene unalibe chiyambi kapena sudzakhalanso konse ndi mathero, ndi wanga ndi wanu mwa chisomo cha Mulungu mwa Yesu Khristu. Ndi zimenezotu.

¹³⁹ Tsopano, “gehena,” ife tibwerera kwa izo kwakanthawi. Ine ndikukuuzani inu kuti—kuti sipangakhale... Ine ndimakhulupirira mu gehena woyaka moto. Inde, bwana, Baibulo linanena chomwecho, nyanja ya moto. Tsopano, koma iyo siingakhale ya nthawizo... iyo siingakhale Yamuyaya. Izo zitha kutero... Baibulo silimanena konse kuti ndi Wamuyaya, Ilo limati “wosatha” gehena. Silimanena mawu akuti Muiyaya, ilo limati “wosatha” gehena. Tsopano, iye anakonzedwera mdierekezi ndi angelo ake; gehena wosatha, osati Wamuyaya. Tsopano, zitatha... Solo imeneyo ikhoza kuzunzidwa pamenepo chifukwa cha zomwe amachita kwa zaka teni milioni, kwa zonse zimene ine ndikudziwa. Ine sindikudziwa chimene chingakhale *chosatha* pamaso pa Mulungu. Izo zikhoza kukhala kwa maminiti faivi, mwina kwa zaka milioni, mwina kwa zaka mamilioni teni, koma idzafika nthawi pamene mzimu umenewo sudzakhalanso.

¹⁴⁰ Apa ndi izi zimene Baibulo linanena, onani:

...Iye amene alakika sadzapwetekedwa ndi imfa yachiwiri.

¹⁴¹ Imfa yoyamba ndi kulekanitsidwa ndi okonedwa athu. Ife tikupita mu Kukhalapo kwa Mulungu, osadzachokanso mu Kukhalapo Kwake. Mukuona? Tsopano, ngati pali imfa yachiwiri, ndiye imeneyo idzayenera kukhala imfa ya moyo. Ndiyeno iye amene aligonjetsa dziko lapansi, kapena agonjetsa zinthu za mdziko, ali nawo Moyo Wamuyaya ndipo sadzakhudzidwa konse ndi imfa yachiwiri. Ndi zimenezotu, Moyo Wamuyaya. Koma wo—wochimwayo... Baibulo linati, “Mkazi amene amakhala mchisangalalo ndi wakufa ali ndi moyo.” Kulondola uko? “Moyo umene uchimwa, iwo udzafa ndithudi.” Kodi *kufa* ndi chiyani? Kwathunthu “kulekana,”

“osakhalaponso.” Mukuona? Tsopano, ndi kudulidwa, kulondola. Kudulidwa, osakhalaponso kalikonse kwa izo. Zidzatenga nthawi yaitali bwanji kutenga zimenezo? Iwo udzadzutsa kachitidwe komweko komwe iwo unaloweramo, ndipo iwo udzafika pamalo pamene sipadzakhala kalikonse kotsalira ka iwo. Iwo udzangobwerera kuchokera komwe iwo unapangidwako.

¹⁴² Ife tikhoza kutenga kakhungu, ndi kukaswa kakhunguko kukhala khungu limodzi, kupita ku khungu lina, mpaka inu mukhoza kutsikira ku khungu loyambalo; kuswera mu khungu limenelo, mukatero ndiye kuti mwapeza mmene magazi amapangidwira; inu mumabwera mu mapangidwe osiyanasiyana a magazi, ndiyeno inu mumatsikira ku gawo laling'ono mu khungu limenelo: ndiwo moyo. Iwo sangakhoze kuzipeza zimenezo. Iwo samadziwa kanthu ka izo. Tsopano, moyo umenewo potsiriza udzafika pa malo mpaka sudzakhalaponso; chirichonse chimene chiri mapangidwe a moyo umenewo, ine sindikukhulupirira kuti uli ndi mapangidwe aliwonse. Izo zingakhale zauzimu.

¹⁴³ Ndiyeno, mmenemo, pamapeto pake zidzasiyana kwathunthu ndipo sizidzakhalaponso. Ndi zomwe Baibulo linanena, “Moyo umene uchimwa, iwo udzafa.” “Ndipo iwo amene agonjetsa mu mibadwo ya mpingo iyi kuno sadzapwetekedwa ndi imfa *yachiwiri*.” Thupi limayamba kufa, solo imadzafa kenako ndipo siidzakhalaponso. Mukuona? Ndizo...kodi inu mukukhulupirira kuti limenelo ndi Baibulo limene limanena zimenezo?

¹⁴⁴ Tsopano kumbukirani, ngati gehena ali Wamuyaya, ndiye kuti Baibulo likulakwitsa pamene linati “gehena anachita kulengedwa.” Ndiyeno ngati munthu ati akapsye Kwamuyaya, mu gehena, ndiye kuti iye adzayenera kudzakhala ndi Moyo Wamuyaya kuti adzakhale maso, kuti adzapsye. Nkulondola uko? Chabwino, ndi mitundu ingati ya Moyo Wamuyaya yomwe ilipo? Umodzi. Uko nkulondola. Moyo Wamuyaya umodzi wokha.

¹⁴⁵ Tsopano, musachokepo ndi kuti, “M'bale Branham sakhulupirira za gehena.” M'bale Branham amakhulupirira za gehena. Baibulo limaphunzitsa kuti ilipo gehena. Motsimikiza basi monga alipo ma—malo opumulira, alipo malo a—a chilango. Ndipo Mulungu ndithudi adzapangitsa kuti moyo umene ukumuchimwira Iye udzalangidwe. Ndi chifukwa chomukana Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wako, iwe ndithudi udzalangidwa chifukwa cha zimenezo. Koma idzakhalapo nthawi imene inu simudzakhalaponso. Koma kodi zaka milioni zingati zomwe zidzatenge kuti inu mudzabwerere kwa izo, ine sindikudziwa. Koma nthawiina . . .

146 Ndinu munthu wa nthawi kufikira inu mutabadwanso kachiwiri, mukadzatero mudzakhala munthu Wamuyaya. Ndipo njira yokhayo yomwe inu mungawupezere Iwo ndi kukhala ndi gawo la Mulungu mwa inu, kukhala Moyo Wamuyaya. Kodi inu mukuziwona zimenezo? Ndithudi.

*Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene
Mzimu ukunena kwa mipingo; . . .*

147 Ine ndimamkonda Iye. Sichoncho inu? Ndine wokondwa kwambiri kukhala nawo Moyo Wamuyaya. Zimenezo sizindivutitsa ine nkomwe, chifukwa chakuti ife tiri nawo Moyo Wamuyaya tsopano. Ndipo ine ndikudziwa zimenezo, ndipo ine ndikudalira kuti aliyense akhala nawo Iwo, tonse a ife.

148 Ireniasi, inde, ine ndinali ndi cholemba apa pa Ireniasi, kuti, “ndiwerenge mbiriyakale iyi.” Chifukwa chomwe Ireniasi anasankhidwa ndi chifukwa chakuti iye anali ndi zizindikiro za Mpingo (woyambirira) wa Pentekoste ukumutsatira iye.

149 Tsopano, ngati Mulungu. . . Ndi angati amakhulupirira kuti Mpingo unayambira pa Pentekoste? Chabwino. Ndi angati amakhulupirira kuti Mulungu anawuvomereza Mpingo pa Pentekoste? Chabwino, bwana. Ndiye ngati umenewo unali Mpingo woyamba wa Mulungu, ndipo ndi chimene Iye anawutcha “Mpingo,” ndipo Iye ndiye Mpesa tsopano, ife ndife nthambi, ngati Mpesa udzayike konse nthambi ina, kodi iyo idzakhala chiyani? Pentekoste. Eya! Tsopano, mwinamwake osati mwa dzina. Tsopano ife tiri nawo *maina* a Pentekoste, koma zimenezo sizoposa Methodisti, Baptisti, Presbateria, Pentekoste. Zimenezo sizitanthauza kanthu, mwawona, ilo ndi dzina chabe. Koma bola ngati inu muli ndi Chokuchitikirani mu mtima mwanu cha Chipentekoste, Pentekoste mu solo yanu, kukupatsani inu Moyo Wamuyaya, ndiye Mulungu wakulonjezani inu kuti, “Inu simudzakhudzidwa konse ndi imfa yachiwiri;” kuti, inu muli nawo Moyo Wamuyaya ndipo *simungathe* kukhudzidwa ndi imfa yachiwiri. Mukuona? Inu muli. . . ndinu. . .

150 “Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu.” Tsopano, musawukwiyitse Iwo (kuchita zinthu zosayenera). Ngati inu mutero, mudzalipira izo; chifukwa Baibulo linati, “Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Nkulondola uko? “Musawukwiyitse Mzimu Woyera.”

151 Oh! Lidzakhala tsiku lodabwitsa, mmawa wina, zina za nthawi izi. Kutu ndikuwonetseni inu kuti chiwukitsiro chidzakhala cha konsekonse, “Padzakhala awiri mmunda, ndipo Ine ndidzatenga mmodzi; ndi awiri pa bedi, ndipo ine ndidzatengapo mmodzi.” Mwawona, udzakhala usiku malo amodzi, ndi masana mbali ina ya dziko lapansi; chidzakhala chiukitsiro cha konsekonse, Mkwatulo umenewo. Lipenga la

Mulungu lidzawomba, ndipo mmodzi aliyense wa awa, a mpingo wawung'ono uwu *apa, apa, apa*, ndipo ngakhale gulu laling'ono ilo lomwe linadutsa *pamenepo*, ndi kubwera kunja *kuno, apa, apa*.

¹⁵² Pamene namwali ameneyo, namwali ameneyo pamene iye anawona mu ulonda wa chisanu ndi chiwiri umenewo... Tsopano, kumbukirani, panali anamwali asanu ndi awiri. Nkulondola uko? Kapena, ine ndikutanthauza, anamwali asanu anapita panja... Anamwali khumi anatuluka panja kukakumana ndi Ambuye, asanu anali ochenjera ndipo asanu anali opusa. Nkulondola uko? Ndipo tsopano, mmaulonda ngakhalebe, panali maulonda asanu ndi awiri. Ndipo kumapeto kwa ulonda wachisanu ndi chiwiri (ena anagona ku ulonda *uwu, uwu, uwu, uwu*, ndi *uwo, . . .*), ulonda wachisanu ndi chiwiri, panamveka mfuu, "Taonani, Mkwati akubwera, pitani inu panja mukakumane naye Iye." Ndipo iwo anawuka ndipo anakakonza nyali zawo. Ndipo ena onse awa anadzuka kudutsa *apa*. Oh, imeneyo siidzakhala nthawi yodabwitsa!

Oh, ife tinkakonda kuyimba nyimbo yaying'ono:

Ndi nthawi yodabwitsa kwa inu,
Nthawi yodabwitsa bwanji kwa ine;
Ngati tonse tikukonzekera kukumana ndi Yesu
Mfumu yathu,
Idzakhala nthawi yodabwitsa bwanji.

Apa, tiwone ngati ife tingaiyimbe iyo:

Nthawi yodabwitsa bwanji kwa inu,
Nthawi yodabwitsa bwanji kwa ine;
Ngati ife tonse titakonzekera kudzakumana
naye Yesu Mfumu yathu,
Idzakhala nthawi yodabwitsa bwanji. (Kodi
izo sizidzakhala zodabwitsa?)

Oh, sizidzakhala zodabwitsa kumeneko,
Opanda zolemetsa zonyamula?
Kuimba mokondwera ndi mabelu a mtima
wonse akulira,
Oh, sizikakhala zodabwitsa kumeneko?

¹⁵³ Ndi angati a inu amene mukudziwa kuti mukafika kwanu? Ndi angati mukudziwa kuti mutuluka pa khomo apo? Inu simukudziwa. Ndi angati mukudziwa kuti mukatuluka kunja inu mudzabweranso muno? Inu simungakhoze kudziwa. Chotero musalole usiku uno ulephere; inu musamulephere Mulungu mu usikuuno, chifukwa uwu ukhoza kukhala usiku wotsiriza womwe inu mudzakhale ndi nthawi kapena mwayi. Kodi ndinu ndani, mulimonse? Kodi inu munachokera kuti? Kodi inu mukupita kuti? Buku lokhalo padziko lapansi limene lingakuuzeni inu chimene icho chiri, ndi Baibulo lakale lodala

ili pano. Ndipo ndiro Baibulo lomwe ife timalikhulupirira, ndiye Mulungu amene ife timamukhulupirira.

154 Ndipo ngati inu simuli mwa Mkwatibwi ameneyo, mu gulu laling'ono ili la apang'ono, kutali komwe *kuno* lero kufinyidwa kunja ndi tizikhulupiriro ndi zipembedzo, ndi zina zotero, ngati—ngati—ngati inu simuli mu gulu laling'ono limenelo... Tsopano, inu simukusowa kujowina kachisi uyu, inu simukusowa kujowina chirichonse, inu mukungosowa kuti mubadwire mu Ufumu umenewo. Tsopano, ngati inu mukufuna chiyanjano chanu mu Methodisti, Baptisti, Presbateria, kulikonse kumene inu mukufuna icho, izo ziri ndi inu. Mwaona, inu mukayike chiyanjano chanu ndi aliyense yemwe inu mukufuna kutero. Koma ine ndikuuzani inu chinthu chimodzi: pamene inu mwabadwa mwatsopano, inu mukudziwa, “mbalame za nthenga...” Mai!

155 Winawake anandifunsa ine nthawi ina, anati, “M'bale Branham, inu munawauza anthu amenewo, 'Bwererani ku tchalitchi cha Methodist.’”

Ine ndinati, “Ndithudi. Asiyeni awaponyere iwo kunja, ndipo iwo alibe malo oti apiteko.” Chotero ndiye ife tidza...

Ziri bwino, bwererani, sizikhala motalika kwambiri, inu mwawona. Izo sizitenga nthawi yayitali kwambiri, iwo adzabwereranso kachiwiri.

156 Mukudziwa, nthawi ina mu... Nowa... chombo, malo achitetezero, Nowa, kunachitika chigumula chachikulu chinabwera. Ndipo chotero Nowa anamutulutsa khwangwala kuchokera mchingalawa, ndipo iye anangopita kumakangolira ndi kumangoyang'ana pozungulira. Bwanji, iye anakhutitsidwa, chifukwa iye anali khwangwala kuyamba ndi kuyamba. Iye amakhoza kuwuluka kuchokera pa nyama imodzi yakufa, ndi kumadya mpaka kukhutu mphongolo iyi, ndi kupita cha uko pa izi—pa nkhoa yakale iyi ndi kukadya mpaka kukhuta iyo, ndi china chakensa, kumene kunali basi mitundu yonse ya mitembo yakufa itagonaponse.

157 Chotero khwangwala amangokhala pansu pamenepo ndi kumalira, “Mnyamata, ine ndiri ndi phwando ndekha ndekha!” akungolira kumeneko.

158 Koma pamene iwo anaitulutsa nkunda yaying'ono iyo, iye anali chikhalidwe chosiyana. Kununkha kumeneko, iye “sakanakhoza kupirira izo. Hmm!” Chifukwa chiyani? Nkhunda ilibe ndulu iliyonse; ndi mbalame yokhayo yomwe ilibe ndulu. Iyo siikanatha kugaya zimenezo, chotero chinthu chokhacho chomwe iye akanachita ndi kubwerera mchingalawa ndi kukagogoda pakhomo.

159 Kungopita kulikonse komwe inu mukukufuna. Chinthu chokha chomwe ine ndikukupemphani inu kuti muchite ndi kungolowa mu Ufumu, ndipo ine ndikudziwa komwe inu

mudzapite. Inu simudzatha kupirira izo aponso, m'bale, inu mudzati, "Ine ndadutsa mzere wolekanitsa, ine ndalisiya dziko lino kumbuyo." Inde, bwana. Ndithudi izo ziri.

Oh, anasonkhana mchipinda chapamwamba,
Onse akupemphera mu Dzina Lake,
Anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,
Ndipo mphamvu yotumikira inabwera;
Tsopano chimene Iye anawachitira iwo tsiku
limenero

Iye adzakuchitirani inu chomwecho,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo. (Sichoncho inu?)

Mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena...
mmodzi wawo; (Aleluya!)

Mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo.

Ndi angati amene akukondwera nazo izo usikuuno? Oh, mai!

Bwera, m'bale wanga, ufune mdalitso uwu
Umene udzatsuke mtima wako kwa tchimo,
Umene udzayambitse mabelu achisangala
kulira

Ndi kuika moyo wako pamoto;
Oh, mukutantha tsopano mkati mwa mtima
mwanga,

Oh, ulemelero kwa Dzina Lake,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena...
mmodzi wa iwo.

Ndine mmodzi wawo, ndine mmodzi wawo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena...
mmodzi wawo; (Aleluya!)

Mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo.

¹⁶⁰ Tsopano pamene ife tikuimba ndime yotsatira iyi, ine ndikufuna inu kuti mugwirane chanza, monga inu mumachitira usiku uliwonse, Amethodisti onse, ndi Abaptisti, ndi Apresbateria. Mugwirane chanza wina ndi mzake, ndipo mukhale okondana mokwanira kuti mukhoza kutafuna chingamu cha wina ndi mzake, ngati inu mungathe. Tsopano mungokhala enieni, ochezeka kwenikweni, ochezeka tsopano pamene ife tikuyimba iyo:

Ndine mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo;

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo.

Ngakhale anthu awa angakhale osaphunzira,
Kapena obwekerera za chuma cha mdziko,
Onse analandira Pentekoste wawo,
Anabatizidwa mu Dzina la Yesu;
Ndipo iwo akunena tsopano, kutali ndi
motalika,
Mphamvu Yake ndi yomweyo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena. . .

Tsopano tiyeni tiimbe iyo kwenikweni:

Oh, mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena. . .
mmodzi wawo; (Aleluya!)
Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo.

¹⁶¹ Kodi mungakhale wololera kukhala wofera wa Iye ndi Asmurna? Ngati zitafika pamalo oti muyenera kuyang'anizana ndi imfa kapena kubweza izo, kodi mungayang'anizane nayo? Inde, bwana. O Mulungu, icho chingakhale chosangalatsa. Inde, bwana. Umo ndi momwe ndimafunira kupita, paguwa pomwe pano. Uko nkulondola. Ine ndimaganiza kuti ndapezana nazo izo ndipo iwo anali oti achita izo mu Germany kuno osati kale kwambiri. Oh, iwo anali oti andiwombere ine kudzera muyezo wa usiku, ndipo asirikali aku Germany anathamanga kudzandizungulira ine paliponse ndi kudzaimitsa monga *choncho*. Ine ndinaganiza, "Chingakhale chinthu chodabwitsa bwanji kufera Mbuye wanga pomwe pano mmunda." Oh, mai! Chiyani—ndi chinthu chodabwitsa bwanji.

¹⁶² Chabwino, ndiloleni ine ndikuyimbireni nyimbo yaying'ono. Ine ndingathe? Kodi inu muli nayo—kodi inu muli nayo nthawi ya ina yaing'ono chabe? Chabwino. Ine sindimatha kuyimba, ine ndimayankhula iyo. Oh, ine nthawizonse ndakhala ndikufuna kuyimba. Ndipo ena a masiku awa mukadzafika kunyumba yanu yokongola yaikulu kumwamba kumeneko mu Paradaiso, kumapeto kwenikweni kwa nkhalango kumusi uko, komwe Russell Creech ndi ine tidzakhala tikusaka, inu mukudziwa. Kumapeto kwa nkhalangoko kudzakhala kanyumba kakang'ono kumeneko kamene M'bale Neville amakayimba, *Mudzandimangire Ine Kanyumba pa Ngodya*, (ine ndimaganiza kuti iye amanena za malo anga.) *ku Dziko la ulemelero*. Umodzi wa mmawa awa pamene inu muzidzapita kunja pa khonde lanu lalikulu kumeneko, ndi kudzayang'ana pamenepo monga chomwecho, Kutali kumusi uko pa kona mudzamumva wina akuyimba:

Chisomo chodabwitsa! kumveka kwake
kokoma bwanji,
Chimene chinapulumutsa wopandapake
wonga ine!

¹⁶³ Inu mudzati, “Chabwino, akudalitseni Mulungu, M'bale Branham wakale wakwanitsa kufika. Ndi ameneyo, ndikumumva waimirira kumeneko pompano, akuyimba *Chisomo Chodabwitsa.*”

¹⁶⁴ Chidzakhala chisomo chodabwitsa chimene chinandibweretsa ine kumeneko. Uko nkulondola.

Koma ukuwukha magazi, inde, (Ndi chifukwa chake ine ndikulalikira Izi.) uwukukha magazi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha magazi,
Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukukhalira kuwukha magazi.

Woyamba kufera dongosolo la Mzimu Woyera ili,

Anali Yohane Mbatizi, koma iye anafa ngati munthu;

Kunako kunadzabwera Ambuye Yesu, anampachika Iye,

Iye anaphunzitsa kuti Mzimu ukanadzawapulumutsa anthu ku tchimo.

Panali Petro ndi Paulo, ndi Yohane wauzimu, Anapereka miyoyo yawo kuti Uthenga uwu uwale;

Anasakaniza magazi awo, monga aneneri akale,

Kuti Mawu owona a Mulungu akhoze kunenedwa moon.

Pali miyoyo pansu pa guwa, (oferi awa,) akulira, “Mpakana liti?”

Kuti Ambuye awalange iwo amene achita zoipa; (Mvetserani! Mwachangu!)

Koma adzakhhalapo ena ochuluka ati adzapereke moyo wawo wa magazi

Chifukwa cha Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ndi kusefukira kofiira.

Ukuwukha magazi, inde, ukuwukha magazi, Uthenga wa Mzimu Woyera ukuwukha magazi, Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi, Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukungokhalira kuwukha magazi.

¹⁶⁵ Oh, padzakhala pali . . .

[Mlongo ayankhula mu lirime lina, m'bale akupereka kutanthauzira. M'bale akuyankhula mu chinenero china, mlongo akuyankhula mchinenero china. Malo opanda kanthu pa tepi. M'bale apereka kutanthauzira—Mkonzi]. Ulemerero. Ameni. Ameni. Hmm. Hmm. Ulemelero. Ameni. Inde.

¹⁶⁶ Ameni. “Iye amene ali nalo khutu, msiyeni iye amve chimene Mzimu ukuyankhula kwa mipingo.”

Ine ndinkonda Iye. . .

Tipembedze tsopano, tiwone zomwe Iye ati achite. Ngati inu simunayambe mwamukondapo Iye, kodi inu mungafune kumukonda Iye tsopano? Kodi inu mungaimirire ndi kumuzindikira Iye, kumutenga Iye ngati Mpulumutsi wanu?

. . . ine, (Mulungu akudalitseni inu, m'bale.)

Ndipo anagu. . .

Winawake aimirira, ndikuti, “Ine ndikumufuna Iye, pakali pano, ine ndikufuna kuti ndimukonde Iye”?

. . . Chipulumutso

Pa wa Kalvare. . .

Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, dona wamng'ono.

Ine ndinkonda Iye. . .

Iye amene ali ndi khutu, msiyeni iye amve chimene Mzimu anena kwa mpingo.

. . . Iye anayamba kundikonda ine

Nandigula chipulumutso changa

Pa mtengo wa Kalvare.

¹⁶⁷ Atate athu Akumwamba, pamene Inu mukuwawona atatu awa ataimirira ku mapazi awo, O Mulungu, Ine ndikukupemphani Inu kuti muwachitire chifundo, O Wamuyaya Uyo, ndi kuwapatsa iwo chikhululukiro cha tchimo lililonse, ndi chipulumutso, Mzimu Woyera mmoyo wawo, kuti iwo asadzakhudzidwe ndi imfa yachiwiri. Iwo akuzindikira, Ambuye, usikuuno, pamene iwo ayima pamenepo, kuti—kuti pali chinachake chayandikira. Mzimu Woyera wapereka chenjezo. Kuwuwona Mzimu wa Mulungu ukugwira ntchito pakati pa anthu, kuwuwona Iwo ukugwira ntchito molingana ndi Malemba, basi mauthenga atatuwu ndi kutseka. O Mulungu, uthenga kwa munthu aliyense.

¹⁶⁸ Tsopano, Atate, ife tikukupemphani Inu kuti mutichitire chifundo. Mulole Mzimu wofunika uja ukhale pakati pathu. Mulole ife tiwulemekeze Iwo, Mulungu; perekani izi. Itengereni miyoyo iyi mmanja Mwanu, Atate, iwo ndi zipatso za Uthenga usikuuno, ndi za uthenga wochokera kwa Mzimu Woyera womwe unalankhulidwa pakati pathu. Ndipo ife tikupempha, Atate Mulungu, kuti Inu mukhale nawo iwo masiku onse a moyo wawo.

Ndipo mulole “mdziko losatha” mulole ife tikakomane nawo iwo mmenemo, opulumutsidwa ndi Magazi ndi chisomo cha Khristu. Ife tikuwapereka iwo kwa Inu tsopano, Atate, adzazeni iwo ndi Mzimu Wanu Woyera. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

¹⁶⁹ Mulungu akudalitseni inu, abale anga. Aliyense yemwe ali pafupi ndi anthu amenewo amene anaimirira, Akhristu, agwireni chanza chawo pamene iwo akhala pansu, apatseni iwo . . . muwafunire iwo liwiro la Mulungu.

¹⁷⁰ Mukuwona momwe Mzimu Woyera umakhalira womvera, momwe Iwo umachitira izo pa mapeto pomwe? Mukuona? Baibulo linati, “Mulole . . . iwo amene amayankhula ndi malirime akhale awiri, kapena ayi . . . asapitirire atatu,” inu mwawona. Uthengawo osati pamene ine ndinali kuyankhula, izo zonse zitatha. Umo ndi momwe zimayenera kukhalira, aliyense molemekeza kwenikweni ndi kumamvetsera zomwe Mzimu ukuyankhula. Ndiye chinachitika ndi chiyani? Ochimwa anadzuka kuti alape. Oh, taganizani. Mzimu Woyera Iwowokha, osamvetsa izo . . . ngakhale kudzera mu Mawu, wabwera ndipo wapanga kuwonetsera.

¹⁷¹ Ine ndikudziwa ena a anthu awa omwe akuyankhula mmalirime, ine ndikuwadziwa atatu onse a iwo amene anayankhula; ndipo ine—ine ndikuwadziwa iwo amene anapereka kutanthauzira; ine ndikudziwa moyo wawo wopanda tchimo pamaso pa Mulungu. M'bale Neville pano, m'busa wathu, mtumiki wa Methodisti; ameneyo ndi mtumiki wa Methodisti, wakhala apa, analandira Mzimu Woyera. Junie, cha apa, M'bale Jackson, mlaliki wina wa Methodisti, analandira Mzimu Woyera. Uko nkulondola, ndi mphatso ya malirime ndi kutanthauzira.

¹⁷² Ndipo inu mukuzindikira momwe ife timakhalira mu mpingo, aliyense molemekeza; Mulungu akamayankhula. Inu mukuwona momwe Iye amayankhulira ndendende basi mogwirizana ndi Baibulo; umodzi; uthengawo sumafika bwino bwino, Iye amadzayankhulanso iwo, koma Iye sangayankhule koposera katatu; mwawona, molingana ndi Malemba pamenepo. Mwaona, Iye amapereka uthenga umenewo; Iye samazikolakola izo, “pakuti mzimu wa aneneri umamvera mneneriyo.” Chirichonse chimamvetsera ndiponso mwakachetechete . . .

¹⁷³ Tsopano ndi momwe mpingo uyenera kukhalira mu dongosolo. Tsopano kwa inu anthu omwe muli pano mukuchokera kunjani, amene mwandimvapo ine ndikuyankhula izo, ndi momwe zimayenera kukhalira. Mwaona, uthengawo ukamapita. Muziwona zotsatira? Izo zimachitika nthawi yomweyo. Chinachake chimachitika, ndendende basi monga kuzindikira za mumtima kapena mzimu wina uliwonse. Kodi Iye siwodabwitsa? Oh, ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti chinthu chomwecho chimene chinadzozedwa ndi Paulo

Woyera, chiri pomwe *pano*, sichinafe chafika mpaka pomwe *apa*. Chikadali chinthu chomwecho. Oh, ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti ndine mmodzi wawo. Sichoncho inu? Chabwino.

¹⁷⁴ Tsopano, mawa usiku ikamati seveni koloko, ife tikutenga m'badwo wa Laodikaya, ndipo umenewo ndi m'badwo wa *chikwati*. Ine ndikufuna kuti inu mubwere ngati inu mungathe. Ine ndinachedwerapo pang'ono usikuuno, chifukwa mwinamwake Mzimu Woyera ukuyankhula ndi zina zotero. Koma ndi molawirirabe, kwangotsala pafupifupi maminiti twente okha itadutsa naini. Ndipo kawirikawiri ine ndimakhala ndiri pano teni kapena leveni koloko, chotero uko ndi kulawirira kwenikweni kuno. Chotero kodi inu mukusangalala ndi—ndi—ndi mauthenga a Ambuye? Inu mukuterodi? Iwo ukudyetsa solo yanu.

¹⁷⁵ Mulungu akudalitseni inu, ana anga. Inu mukudziwa, ine ndimakukondani inu ndi mtima wanga wonse. Ndipo nthawizina pamene Mzimu wandigwira ine, umadula konse konse. . . Umo ndi mmene Mawu amakhallira, Iwo ndi akuthwa ngati lupanga lakuthwa konsekonse. Iwo amadula akamabwera, akamapita, mkati, kunja, mbali iliyonse. Koma ndi zomwe zimatudula ife. Mdulidwe umangodula mnofu wotsalira, zinthu zimene ife sitimayenera kukhala nazo.

¹⁷⁶ Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire. Kodi inu mwawumva Mzimu pa kutanthauzira usikuuno? “Musiyе zopusa zimenezо!” Iwo umadula. Mukhale owona mtima! Ife tonse timachoka pamzere, koma Mulungu amadziwa momwe angadulire ma bampu kuchoka pa ife. Sichoncho Iye? Iye ndithudi amatero. Ndine wothokoza chifukwa cha izo. Sichoncho inu?

¹⁷⁷ Kodi ndinu walimba wamng'ono pano? Ine sindikuwona. . . Ndi Teddy. . .? Ine sindikumuwona iye pano paliponse. Ndi—kodi ichi ndi. . .? Chabwino, mlongo, ngati inu mungathe. Kodi ameneyo ndi mwana wanu wamkazi, M'bale Daulton? Mpongozi wamkazi. Chabwino. Dona wamng'ono wamphamvu wabwino, wokondwa kwambiri kuti ndinu Mkhristu. Chabwino, kodi nyimbo yathu yabwino, yakale yotulukira ija ndi chiyani? Tiyeni tiyese imodzi, ife tisanatero, tsopano. Miniti yokha, mlongo, ife tisanayimbe *Tenga Dzina La Yesu Pamodzi Ndi Iwe*.

¹⁷⁸ Ndi angati amaidziwa kuti *Musaiwale Pemphero Lapabanja*? Ndi angati amapemphera m'banja mwanu, banja lanu limapemphera? Oh, izo nzabwino. Tiyeni tiyiyese iyo kamodzi, monga a nthawi zakhale tsopano:

Musaiwale pemphero la pabanja,
Yesu akufuna akakumane nanu uko;
Iye adzasamalira nkhawa zanu zonse,
Oh, musaiwale pemphero la pabanja.

Inu mukuikonda iyo? Tiyeni tiyeesenso iyo:

Musaiwale pemphero la pabanja,
 Yesu akufuna akakumane nanu kumeneko;
 (Muli ndi tsiku, tsopano.)
 Iye adzasamalira nkhawa zanu zonse,
 Oh, musaiwale pemphero lanu la pa banja.

179 [Mlongo akuti, “M’bale Branham, kodi ine ndinganene chinachake?”—Mkonzi]. Ndithudi mukhoza, Mlongo. [Mlongo akuyamba kuyankhula. Malo opanda kanthu pa tepi.] Mlongo Nash, nzabwino kwambiri zimenezo. Oh, ngati mutangoti:

Ngati titangodalira ndipo osakaikira, Iye
 ndithudi adzakupyoletsani;
 Ingotengerani katundu wanu kwa Ambuye
 mukamusiye iye kumeneko.

Tulani, tulani,
 Tengerani katundu wanu kwa Ambuye;
 Ngati tingadalire ndipo osakaika, Iye ndithudi
 adzakupyoletsani;
 Tengerani katundu wanu kwa Ambuye.

180 Kodi inu simumazikonda nyimbo zakale izo? Oh, ine basi . . . Ine ndikukhulupirira amuna amenewo amatola cholemba ndipo amawuziridwa ndi Mzimu Woyera kuti awerenge izo.

181 Monga Fanny Crosby wakhungu pamene anthu achidziko amenewo a tsiku limenelo ankayesetsa kuti amupange iye alembe nyimbo zachidziko, anati, “Bwanji, iwe udzakhala mkazi wolemera.”

Iye anati, “Ine ndawupereka moyo wanga kwa Khristu, ndi luso langa lonse.” Iye anali wakhungu, inu mukudziwa. Anati, “Ine—ine ndikuwupereka moyo wanga ndi zonse kwa Khristu.” Iye anati . . .

182 Ndipo kenako iwo anakhumudwa ndi iye chifukwa iye anakana mwayi woterowo. Iye sanagulitse mafulu ake akubadwa monga Bambo Presley ndi iwo anachitira, koma iye—iye anakhalabe wokhulupirika. Chotero iye—iye . . . Iwo—iwo anamusiya iye, anati, “Ndiye iwe ukadzafika Kumwamba, akakhalako malo oterowo,” anati, “ngati iwe uli monga iwe uliri kuno, ukakhala wakhungu.” Anati, “Bwanji ngati iwe *utadzakhalako* wakhungu,” anati, “iwe ukamudziwa bwanji Iye?”

Iye anati, “Ndidzamudziwa Iye. Ndidzamudziwa Iye.”

Anati, “Bwanji ngati iwe utakakhala wakhungu? Bwanji ngati iwe *utadzakhalako* wakhungu?”

Iye anati, “Ine ndidzakhudza zipsyera za misomali.” Kenako iye anatembenuka, iye anayamba kubwerera mmbuyo, ndipo iye anati:

Ndidzamudziwa Iye, ndidzamudziwa Iye,
 Ndipo powomboledwera kumbali Yake ine
 ndidzaima;
 Ndidzamudziwa Iye, ndidzamudziwa Iye
 Ndi zipsyera za misomali mdzanja Lake.

183 O Yesu wanga, ndi zipsyera zisanu zamtengo wapatali zimenezo, kukhetsera magazi ine kutsidya, ine ndingakhoze bwanji kumukana Mmodzi wofunika uyo? Ndiroleni ine ndife, ndiroleni ine ndipite ku...Ndiroleni ine ndipite njira ya chirichonse, koma musadzandilole konse kuti ndidzamkane wofunika Uyo yemwe anandifera ine. Inde.

184 Ndipo pamene inu mukuchoka usikuuno, inu mukufuna kuti: *Mutenge Dzina la Yesu Limodzi Nanu*. Chabwino, mlongo. Kodi ife tiime tsopano, tonse pamodzi.

. . . Dzina la Yesu ndi iwe,
 Mwana wachisoni ndi watsoka;
 Lidzakusangalatsa ndi kukutonthoza,
 Litenge Ilo kulikonse upita.

Dzina Lofunika, (Dzina Lofunika!) O nlokoma
 bwanji! (O nlokoma bwanji!)
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba;
 Dzina Lofunika, (Dzina Lofunika!) O nlokoma
 bwanji!
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba.

Tsopano pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, ndi kuyimba mofewa:

Pa Dzina la Yesu kuwerama,
 Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
 Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamveka
 Iye korona,
 Pamene ulendo wathu watha.
 Dzina Lofunika, O nlokoma bwanji!
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba;
 Dzina Lofunika, O nlokoma bwanji! (Lokoma
 bwanji!)
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba.



M'BADWO WA MPINGO WA SMURNA CHA60-1206
(The Smyrnaean Church Age)

MAULALIKI A VUMBULUTSO LA YESU KHRISTU

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachiwiri madzulo, Disembala 6, 1960, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2022 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org